
BOSTON UNIVERSITY
01826 7866

# LINDA MADZI APITE

NIXON MINDANO



BOSTON UNIVERSITY
9 01826 7866

Chi Chewa - Novel MW2030LP 2

# Linda Madzi Apite

Wolemba
Nixon Mindano

Alembi a m'Malaŵi

Popular Publications

BOSTON UNIVERSITY LIBRARIES

Published by:

Popular Publications
P.O. Box 5592
Limbe
Malaŵi.

© Popular Publications 1990

No part of this book may be reproduced in any form, by print, microfilm, or any other means without written permission from the publisher.

Printed in Malaŵi by Montfort Press – Limbe.

BOSTON UNIVERSITY
19 01826 7866

Ch Chewa

## Za M'katimu

PL
8110
C59M56
1990

Mutu 1 Mmera mpoyamba ........ 7

Mutu 2 Tsamba likagwa ........ 16

Mutu 3 Kanthu kali n'khama ........ 24

Mutu 4 Wapsa wa ku tawuni ........ 34

Mutu 5 Linda madzi apite ndiye uziti ndadala ........ 40

Mutu 6 Pano mpakachere ........ 47

Mutu 7 Chaona mnzako chapita mawa chili pa iwe ........ 55

## Mawu oyamba

Zochitika pa moyo wa munthu ndi zambiri. **Linda madzi apite ndiye uziti ndadala,** ndi umodzi mwa miyambi imene timaimva kaŵirikaŵiri. M'bukhu muno mwambiwu, ndayesetsa kuufotokoza mokometsera, pobweretsa mnyamata wina dzina lake Mateyo, amene titha kumulondola bwinobwino.

Phunziro lenileni lomwe mungapeze m'nkhaniyi ndi lakuti: **Muyeso umene umayesa nawo wina, nawenso umadzayesedwa ndi womwewo.** Mateyo atakula movutika, adapita kutawuni nakapeza ntchito pa kampani ina. Pa kampanipo padali a Bwezani, omwe nthaŵi imeneyo adali bwana wamkulu. Iwoŵa nthaŵi zonse ankanyoza anzawo chifukwa cha mpandowo ndi kumaŵachotsa ntchito popanda chifukwa. Mateyo adazunzidwanso ndi a Bwezani mpaka adachotsedwa ntchito. Chifukwa cha khama pa maphunziro, Mateyo adachotsedwa atapambana mayeso a ntchito ndiye sizidamutengere nthaŵi yaitali kupeza ina komwe adakamutumiza ku Mangalande kukachita maphunziro apamwamba. Mateyo adakhala bwana wamkulu atabwerera kumudzi, pamene a Bwezani ntchito yawo idatha kukampani kuja.

Tsiku lina a Bwezani pofunafuna ntchito m'tawuni, chosadziŵa adafika mu ofesi ya Mateyo. Kodi zidaoneka pamenepo nzotani?

Ndikuthokoza mkazi wanga, Rosemary, chifukwa cha chidwi chake nthaŵi yomwe ndinkalemba nkhaniyi. Iye adagwira ntchito pondilangiza zina ndi zina kuti nthanoyi



BOSTON UNIVERSITY
9 01826 7866

ikome chotere.

Sindiyiŵala a Willie T. Zingani, amene kwa nthaŵi yaitali adandiphunzitsa kalembedwe ka nkhani kabwino.

Mayi J.B. Mkandawire a ku Polytechnic, Mulungu aziŵadalitsa chifukwa chondikomera mtima pondilembera nkhaniyi pa tayipi.

Nkhaniyi ndiyopeka. Zonse zomwe zalembedwa sizidachitike. Ngati zidachitikira wina, sindicho chofuna changa kulemba za inu kapena abale anu ngakhale abwenzi anu. Chonde ndikhululukireni.

Kwa inu bambo ndi mayi nditi Mulungu azikutsogolerani chifukwa mudandibereka nkundilera bwino kufikira lero lino. Bukhuli ndi chikumbutso chanu kwa ine.

**Nixon D. Mindano**

BOSTON UNIVERSITY
19 01826 7866

Mutu 1

## Mmera mpoyamba

Dzuŵa lidapendeka, koma kunja kunkatenthabe kotulutsa thukuta. Chifukwa cha kutenthaku, Mateyo ndi bambo ake a Taonana, adakhala pa mthunzi wa mtengo wa mango kuphwetsa mkhuto, komanso kuti kamphepo kozizira bwino kadziŵawombera. Pomwepo a Taonana adayamba kuwodzera, nkumapha tulo tamasana, mkonono ukulindimuka ngati wa mphaka kaya kuti chome wa kutchire. Mateyo adayesayesa kupsinyira tulo m'maso mwake koma timalephereka. Chifukwa cha phokoso la ana omwe ankaseŵera cha pafupi pomwepo, a Taonana adadzidzimuka, Mateyo nkupezerapo mwayi woyamba kulankhula nawo. "Tandiuzani nthano bambo?"

A Taonana asadayankhe pempho lakelo, adayasamula, napukuta thukuta kumaso kwawo. Adamuyang'ana Mateyo kwa nthaŵi yaitali, nawonso nkuliponya funso "Tandiuza nchifukwa chiyani umakonda nthano?"

"Ndimazikonda chifukwa mwagona nzeru ndi phunziro," adayankha Mateyo.

"Basi?"

"Inde ababa. Komanso zimandisangalatsa mukamandifotokozera."

A Taonana adamuyang'ana kunkhope kwake kufikira Mateyo adagwetsa nkhope yake pansi. Pamene a Taonana adayamba kumuuza nthano ya nyama za kuthengo, Mateyo adadzutsa mutu wake, namwetulira. Adasangalala zedi.

"...Dziko likadali mphonje, njovu idali ndi akamwini

ake atatu; mkango, mbawala ndi kalulu. Nthaŵi zonse njovu inkati ikapeza kanthu siinkalephera kuŵagawira akamwini akewo. Tonse timadziŵa kale kudzikonda kwa mkango. Pa banjapo mkango unkadzikonda chimodzimodzi koma chifukwa cha manyazi ndi atatiwo, siunkawonetsera poyera kufikira tsiku lina...", adapuma kaye pang'ono. Luso lolakatula nthano a Taonana adali nalo. Ankati akamafotokoza, ndi momwe iwowo ankayerekezera polankhulapo, zinkampatsa chithunzi Mateyo m'mutu mwake.

"Ndiye zidatani?" adafunsa Mateyo n'chidwi.

"Eya, basi ndiye kenaka njovu idaganiza zofuna kusangalatsa akamwini ake aja koma ganizoli siidaulule msanga kufikira tsulo litafika. Njovu idaŵaitanitsa akamwini ake pamodzi nkungoŵapempha kuti apite kukhola akaphe ng'ombe imodzi. Mkango suudakondwe poganiza kuti atati aja sadaupatse ulemu monga iwo mkamwini woyamba kukwatira pa mudzipo. Iwo unkaganiza kuti tatiwo adayenera kukhazikitsa mkangowo ngati wongoyang'anira.

"Kukholako, mkango nthaŵi zina suunkagwira ntchitoyo, mmalo mwake unkangoima phee pamenepo anzake aja akujijirika ndi ntchito.

"Ntchito yonse itatha, mkango udanama kuti unkadwala mutu ndi cholinga chakuti usasenze nawo nyamayo ndipo mmalo mwake ungonyamula zopepuka monga chikopa ndi ziboda. Anzake aja sadakhumudwe, adasenza koma modzipha kupita nayo nyamayo kunyumba kwa tati... Ukudziŵa momwe zidathera?" adamfunsa a Taonana.

"Ayi bambo tapitirizani," adapempha Mateyo.

"Limeneli likhalepo chenjezo lako. Uyenera kudziŵa kuti phindu la kudzikonda, mwano ndi kaduka ndi kuyipa."

"Inde. Koma tandiuzani kuti zidatani kutha kwake."

"Chabwino. Onse atakafika kunyumba kwa atati, njovu idaŵalamula kuti aliyense atenge katundu wake amene adanyamula kunjira ndipo apite naye kunyumba

kwake kuti akasangalale ndi banja lake. Kodi pamenepa ukuganiza kuti Mkango udawoneka bwanji?" adaliponya funso. Mateyo adangopukusa mutu.

"Kodi uganiza zoterezi kwa ife anthu sizingatichitikire?"

"Eee. Zingachitike bambo chifukwa ena amaganiza kuti angathe kupeza zabwino mosavutikira."

Tsiku limenelo adakamba nkhani zambiri. Kenaka a Taonana adayamba kuyamika khalidwe la Mateyo.

"Inetu bambo sindifuna kuti ndidzakutukwanitseni mtsogolomo ayi paja akutitu moyo uli ngati chithunzi," Mateyo adaŵauza bambo ake.

"Indedi ukunena zoona. Zochita zako zimandipatsa chidwi. Kodi umadziŵa kuti chifukwa cha ntchito zako m'mudzi muno anthu ayambapo kale kukulimbirana kufuna utadzakwatira ana awo?"

"Ayi bambo, sindidziŵa chifukwa ine pakalipano maganizo amenewo ndili nawo kutali ndiponso zodzakwatira m'mudzi mwathu mom'muno ayi."

"Chifukwa chiyani? Umaganizira mtunda uti?"

"Basi kulikonse kumene Chauta adzandilozera."

"Bwinotu chiwona maso nchachabe ungadzagwe nacho m'mavuto. Kukongola nkhope ngati mkuyu sindiye kumene kumamanga banja ayi," adamulangiza a Taonana.

"Ayi bambo. Ngati kukongolanso?"

"Nanga udzadziŵa bwanji za mkazi wabwino mtima pamene n'kale lonse suudamdziŵe chikhalidwe chake?"

Mateyo sadayankhe msanga.

"Basi bambo, nkhaniyi isapite patali."

"Chifukwa? Uyenera kudziŵa zinsinsi zina za pa dziko lapansi. M'moyo wanga uno ndawona anthu ena ambiri amene amakonda mkazi kapena mwamuna chifukwa choti mwina ndi wophunzira bwino, ndi wachuma chambiri kapena apo ayi ndi wobadwa mokongola.

"Za khalidwe la munthuyo alibe nazo ntchito. Mapeto ake amakhala akapolo a munthu mnzake wokhala naye pabanjapo. Banja silitanthauza zinthu ngati zimenezi ayi



BOSTON UNIVERSITY
19 01826 7866

koma chikondi chochokera pansi pa mtima, chikondi chozika mizu yeniyeni choti ngakhale vuto litabwera lotani pa banjapo ngati mafunde a kunyanja, nonse aŵiri mudzayima njii osatekeseka. Wamvapo bwino pamenepo?"

"Inde bambo. Pamenepa mukutanthauza kuti banja ndi mphatso yochokera kwa Mulungu eti?"

"Indedi pamenepa wafunsa bwino. Banja ndi mphatso. Ngati Mulungu akusankhira mkazi kapena mwamuna wa banja, m'banjamo mumapezeka mtendere wosefukira chifukwa Mulungu amamanga matupi anu ngati thupi limodzi. Mudzawona kuti banja lotero, wina akadwala, mnzakeyo sasangalala konse. Nthaŵi zonse akaweruka ku ntchito kaya zakumunda kaya za muofesi amathamangira pa khomo kukamuzonda mnzakeyo. Koma ngati Mulungu sadamange, zonsezi sizikhalapo."

"Kudekha mtima ndiye njira imodzi yofunika eti?" Mateyo ankafunsa mafunso ambiri.

"Inde. Pa moyo wa munthu pafunika kudekha mtima ndiponso kupirira pa zovuta zonse zimene ungakumane nazo pa moyo wako.

"Kukhala bwino ndi anthu, kumvera akuluakulu anu, kusanyoza anzako chifukwa choti iwowo ndi osauka kaya osaphunzira, ndi zinthu zofunikanso kwambiri."

"Mukunenadi zoona bambo. Anthu ena ambiri amanyoza anzawo, anakubala ngakhale akuluakulu chifukwa choti mwina ngophunzira, kapena iwowo ali pa mpando wapamwamba."

Mateyo ndi bambo ake, a Taonana, adaafatsadi kufikira dzuŵa lidaloŵa. Mateyo adali mwana wonyaditsa. Ntchito zomwe Mateyo ankagwira pakhomopo, makolo ake adatsimikizadi mawu aja amati 'kubala kuwombola!' Bambo ake a Mateyo adapuma pa zintchito zina ndi zina. Anthu ambiri adayamika khalidwe la Mateyo. Ku sukulu, Mateyo adali m'banga. Nthaŵi zonse ankakhala nambala wani m'kalasi. Mateyo ankati akatuluka kusukulu ngati palibe ntchito ya pakhomo yofunikira, ankangoti m'nyumba gulubidi, ali pa mabuku

gwii! uyo wayamba kuŵerenga. Atalemba mayeso a sitandade 8, iye adatsimikiza kuti adzapambana. Indedi zidali zoona chifukwa ngakhale aphunzitsi ake nawo ankatsimikiza molingana ndi momwe amapambanira m'kalasimo kuti Mateyo adzasankhidwa kupita kusukulu ya sekondale.

Chauta apatsa moolowa manja kwa iye wolimbika. Zotsatira za mayeso zitatuluka, Mateyo adasankhidwa kupita ku Ziliko Sekondale Sukulu. Makolo ake adasangalala kwambiri. Popeza makolowo ankachita bizinesi ya zigayo ndi masitolo, ndalama zomulipirira Mateyo ku sukulu sizidasoŵe ayi.

Mateyo atafika ku sekondale ya Ziliko adapitiriza khama lake pa maphunziro. Koma vuto lidali loti ophunzira anzake adayamba kumusoŵetsa mtendere ncholinga chofuna kumubwezeretsa mmbuyo. Chifukwa chokonda kuŵerenga mabuku, nthaŵi zonse akakumana naye anzakewo zolankhula zao zinkakhala zonyoza zokhazokha.

"Aŵa ndi a Mateyo basi, achokera mabuku omweŵa pa sekondale pano. Chinyamata sachidziŵa mpang'onong'ono pomwe. Akati kunjoya amangomva anthu," ankatero polankhula ophunzira anzakewo makamaka pamene padali gulu la asungwana, ndiye akatero asungwanawo amvekere pwepwetee kufa nkuseka.

Naye Mateyo akamva zotero amvekere, "Chofunika apa ine ndingosamalapo chomwe ndidadzera pa sukulu pano."

Akatero ankatenga mabuku ake n'kukabisala malo ena n'kumaŵerenga. Chifukwa chakhama lotereli, Mateyo amakhala nambala wani kutha kwa teremu iliyonse. Mateyo adatchukadi kwambiri pa nkhani ya maphunziro, komanso khalidwe lake labwino kwa aphunzitsi ndi anzake ophunzira pa sukulupo, Mateyo anadyadi wani, thu kuopa kupindika. Aphunzitsi adamuyamika Mateyo.

"Mmera mpoyamba," ena mwa aphunzitsi ake ankatero.



BOSTON UNIVERSITY
9 01826 7866

"Indedi. Mtengo ukakhota uli wanthete ndikovuta kuuwongola utakhwima. Monga momwe mukuwonera anyamata enaŵa, ndi okanika ngati namsongole," wina mwa aphunzitsi adatsira ndemanga.

"Koma ine khalidwe la Mateyo ndagoma nalo," mphunzitsi wamkulu adatsira nawo ndemanga. Adawonjezera: "Mbiri yabwino iposa malonda a golide ndi phindu lake liposa siliva." Apa mphunzitsi aliyense adagwedeza mutu kutsimikiza kugwirizana nawo mauwo. "Makolo ena amaganiza kuti kulera bwino kwa mwana nkumangomulekerera pa chinthu chilichonse chimene akuchita. Chomwecho amaiŵala kuti mwanayo akumuphera tsogolo lake," mphunzitsi wina adatero.

"Aponso mwanena mawu owona aphunzitsi," onse adavomereza.

"Mwana ndi mbewu ya mpiru kaya titi mbewu ya chimanga," wina adatero.

"Eya, koma indedi eee... chifukwa ukapanda kusamalira bwino sungathe kukololapo zinthu zambiri."

Aphunzitsiwo adalankhula zambiri zokhudzana ndi makhalidwe osiyanasiyana a ana asukulu. Koma zidaonekeratu poyera kuti kayanjanitso kadachokera kwa Mateyo.

Kuyamba kwa mavuto kudagwa Mateyo ali mu fomu fili teremu yotsiriza. Lidali tsiku Lachitatu nthaŵi ya kummaŵa, piliodi yoyamba maphunziro m'kalasi. Kunja kudacha bwino kwambiri. Nayenso Mateyo tsiku limenelo adasangalala kwambiri. Zidali ngati muja amati "mbuzi ikakondwa amalonda ali pafupi."

Mateyo adali m'banga kaya kuti mtondo pa phunziro la masamu. Iye phunziroli ankalikondadi ndipo mwina ndicho chifukwa chake adasangalala mmaŵa umenewo. Chifukwa chokonda masamu kwambiri ena ankamutchula maina osiyanasiyana omusinjirira.

"Ameneyu dzina lake ndi Mathematishani."

"Ayi, koma kuti mphwake wa Payithogalafe," wina adatero.

"Kodi pamenepa mukutanthauza kuti ndi Galileyo

kapena?" wina adafunsa mwachipongwe.

"Anyamata mukungotaya nthaŵi chabe ndikumalankhula zinthu zopusa mmalo moti muphunzire!" adakalipa Mateyo.

"Eeeee! wakalipa Galileyooo!" onse m'kalasimo adaseka. Koma zoterezi Mateyo sanadandaule nazo. Mtima wake unkangoti zii osagunda mpang'ono pomwe. "Ngati Yesu mwana wa Mulungu adanyozedwa pansi pano chifukwa cha zabwino, nanga kuli bwanji ndi ife anthu olengedwa..." Akatero Mateyo ankalimba mtima nkumangoyankhana nawo anzakewo m'maso muli gwaa, popanda mmanyazi omwe. Pa chifukwa chimenechi anzakewo ankachita manyazi, basi nkusiya kumunenako. Zidali chimodzimodzi mmaŵa wa tsiku limeneli. Aphunzitsi a masamu atoloŵa m'kalasimo anyamata ndi asungwana ena adayamba kumadzuma kumbali. Ena chifukwa chosakonda phunziro la masamu ankachita dala zosokoneza kuti mphunzitsi uja zikamuyipira aŵatulutse panja. Zoterezi zinkachitikadi.

Mphunzitsi uja adaŵalembetsa mayeso a masamu sabata yapitayo. Mateyo adakhonza onse ndipo ndi amene adakhala nambala wani. Wachiŵiri wake adali mtsikana wina dzina lake Selina Kataye ndipo adakhoza sevente pa handedi, wachitatu fote, wachinayi satefaifi, basi enawo adali maziro ndi mafaifi. Ophunzira enawo adatama kuti mayesowo adali okhwima koma Mateyo pachingelezi ankanena kuti 'chikeni fidi' ati kutanthauza kuti padalibe samu yovuta yoti munthu nkugwetserapo thukuta nkuganiza.

Aphunzitsi adamupempha Mateyo kuti apite kutsogolo akalongosolere anzakewo pa bolodi. Akungonyamuka kalasi yonse idakuwa.

"Eeee Galileyoooo! Galileyoooo! Mathematishaniiii!"

Mateyo sizidamkhudze. Chisangalalo chake chidali tsaya. Popita kutsogoloko ankayenda monyadira, pepala lake la mayeso lili kudzanja la manzere. Uja ali pa choko gwi, nkumafotokoza.

"Pamenepa palibe chovuta, funso ili akutanthauza

kuti inuyo mutenge ..." adayamba kulongosola Mateyo. Anzake adangoti kakasi m'kalasimo, ena nkumangogwedeza mitu kukhala ngati kuti adazindikira cholakwa chawo.

M'kalasimo mudali mtsikana wina dzina lake Selina. Iyenso masamu ankawakonda, nthaŵi yomwe Mateyo amafotokoza pa bolodipo, iye ankangomwetulira. Kenaka nthaŵi yomweyo pakhomo pa kalasilo padafika a hedimasitala nampeza Mateyo ali mkati kulongosola. A Hedimasitala adamuyang'ana koma nkhope yawo iri yakugwa. Adaŵaitana aphunzitsi aja panja. Onse m'kalasimo adadziŵa kuti pagwa vuto.

"Tamuuzani Mateyo andipeze ku ofesi," adatero a hedimasitala.

"Pali nkhani yofunikira kwambiri?" adafunsa aphunzitsi modabwa.

"Inde. Tamuuzani afulumire."

Aphunzitsi adamuuza Mateyo kuti aŵatsatire a hedimasitala aja ku ofesi. Aliyense m'kalasimo adali wodabwa. Kodi chifukwa chake chingakhale chiyani? Mateyo amalemba pa bolodi aphunzitsi ali m'kalasimo? Ambiri adafunsa.

"Kaya tizimva tili pompano," ena ankatero.

Mateyo atalowa mu ofesimo, mtima wake ukugundagunda mkati mwachifuwa mwake, adauzidwa kuti akhale pampando. Atakhala pampandopo adawona a hedimasitala akutulutsa kapepala kolembedwapo mawu timizere tiŵiri tokha basi. A hedimasitala adamuyang'ana Mateyo ndi nkhope yokhumudwa. Bulangeti la chisoni lidakuta mumtima mwawo. Pakamwa pawo padauma kuti amulongosolere nkhani yake Mateyo.

"Pepa Mateyo ndiye kuti..." adayamba a hedimasitala ndi mawu odekha. Adapitiriza. "Posachedwa pomwepa ndalandira lamya kuchokera kumudzi kwanu." Adausitsa moyo a hedimasitala. Nayenso Mateyo nthumanzi idamuwomba. Mkamwa moto buu. Kugunda kwa mtima wake kudapitirira. Adatchera khutu Mateyo kuti amvetse bwino.

"Makolo ako achita ngozi. Apa ndikutanthauza bambo ndi mayi ako. Achita ngozi ya galimoto usiku wathawu ndipo onse afera pa malo omwe angoziwo. Kutereku mitembo yawo ili kuchipatala.

"Basi Mateyo. Limba mtima ndiwe munthu wa mwamuna. Pepa ndithu," adayesa kumulimbikitsa. Kulira kuja kudamveka patali. Ambiri omwe adamuona Mateyo akuŵalonda a hedimasitala aja adadzidzimuka kumva chilirocho.



BOSTON UNIVERSITY
19 01826 7866

Mutu 2

## Tsamba likagwa

Zidalidi zoona. Utsi sufuka popanda moto. Anzake a Mateyo pamodzi ndi aphunzitsi aja m'kalasi muja atamva za nkhani yomvetsa chisoniyo onse adatuluka panja kumulondola Mateyo.

"Tikachoka pano tiyende molunjika kumudzi osakhala ku chipatala ayi," adamulongosolera Mateyo a hedimasitala. Anzake ambiri adabwera kudzamupepesa. Koma nthaŵi imeneyi Mateyo saadali woti nkugwirika nkhosi ayi. Ankati akaloŵera uku, kenaka napita uko, kuyang'ana misozi ndi mamina zikungotsika m'masaya. Zidalidi zomvetsa chisoni. Konseko kudali kuzunguzika mwana wa mwini. Mutu wake udawira. Chochita chilichonse pa dziko lapansi lino chidamusoŵa. Dziko lapansi lidaoneka ngati mpira m'manja mwake omwe akadatha kuutembenuzira uku ndi uko posoŵa pothawira.

Mateyo adaona kuti njira ya tsogolo lake idatsekeka tsopano. Adazunzika m'maganizo Mateyo kusamvetsa nkhanza ya moyo wa dziko lapansi.

Aphunzitsi ndi ana onse asukulu adasonkha ndalama zomupepesera. Zonse zidakwana 10 kwacha ndi matambala 50. A hedimasitala ndi aphunzitsi ena kudzanso anzake ena asukulu adampelekeza kwawo.

Pamene ankafika kumudziko, adali madzulo dzuwa litatsamira phiri la Dzonzi. Adakapeza maliro atafika nawo pa khomo kuchokera ku chipatala. Anthu pa khomopo atangomuona Mateyo akubwera potero, adachiutsa chiliro. Ena akugugubudukira kotero, ena uko. Nayenso Mateyo adatsatsalika nacho chiliro.

"Imfa ya mkango mayi! Imfa ya mkango eee nditani bambo! Mwandisiya pa mphepo ine nditanii kalangaaa! Nditsala ndi yani ine bambo? Nkunditsazika komwe ayi Mayi?" Ankati akatero, ngakhale anthu omwe sadali achibale, misozi inkayengeza m'maso mwawo. Ena zotezezi zinkaŵakumbutsa maliro omwe adaŵachitikira kalekale.

M'nyumba ya zovutamo nyimbo za Mulungu zinkaimbidwa. Koma nthaŵi yomwe Mateyo adalowa, aliyense m'nyumbamo adangoti chetee, nyanja ya misonzi itadzala m'maso mwawo.

Mateyo adazunzika kuona makolo ake ali mtulo tosaukanso. Anthu ena ankamuthandiza Mateyo m'maganizo makamaka a hedimasitala ake aja. Adamutengera pambali. "Mateyo, Baibulo litiuza kuti; tisaleke kuyamika Mulungu pa mtendere ngakhale pa mavuto ngati awa. Kodi umakumbukira za nkhani ya Sailasi? Nanga bwanji Yosefe kudzanso Zakaliya?" adamuthandiza a hedimasitala. "Chinsinsi ichi palibe wina aliyense amachidziŵa.

"Usadandaule kuti kodi maŵa ndidzadyanji chifukwa Mulungu adzadyetsa iwe nakusunga ndi moyo. Timamva Mawu a Mulungu akuti tisalire monga anthu otayika koma tikhale nacho chikhulupiriro ndi chiyembekezo mumtima mwathu."

Pamenepo Mateyo adayamba kulimba mtima, makamakanso poganiza kuti chuma chimene adasiya makolo aja chidzamuthandiza pa sukulu yake mpaka kutsiriza. Zonse za maliro zidatha bwino. Ataika maliro, aphunzitsi ndi anzake a Mateyo onse adabwerera ku sukulu koma Mateyo adatsala pambuyo. Itatha sabata imodzi nayenso Mateyo adapita ku sukulu.

Mateyo sadasiye khama lake pa maphunziro, adalimbikira kwambiri podziŵa kuti padalibenso pena podalira koposa sukulu kuti mtsogolo adzaiŵale umasiye akadzakhala pabwino.

Telemu yotsiriza ya fomu fili, Mateyo adapambananso bwino kukhala nambala wani kuyembekezera kuti chaka

chinacho adzayambe fomu folo. Atatsekera sukulu aliyense pasukulupo adabalalika kupita kwawo. Nayenso Mateyo adapita kwawo nakafikira pa khomo pa mayi ake aang'ono, dzina lawo Alekenianene. Nkhani yomvetsa chisoni idali yoti, nthaŵi yomwe Mateyo ankafika kunyumba, adakapeza kuti chuma chonse cha makolo ake chija anthu adagawana kale molimbirana makamaka a kwawo kwa bambo ake. Mateyo kuti ayesere muno ndi muno adalephera.

"Chimenechi ndi chuma cha malume athu!" ena ankatero, ati kumuopsa Mateyo.

"Inenso ndi cha mdzukulu wanga!" ena, diso lili pamtunda ndipo nankanyivwi akutuluka mphepete mwa milomomu.

"Inenso ndi chuma cha achimwene ndiye palibe uyo angati mfwimfwi!" Mateyo adangoti kukamwa kakasi kusowa chochita. Misozi siinkachoka m'maso mwake. Adayesa kuuza akuluakulu aŵa ndi awo kuti amuthandize koma ayi zidali ngati kukolezera moto padzala.

"Ngati finye wina achita mfwimfwi ndi chuma chimenechi atsogola ndithu ndilibe 2 koloko ine!" adawopseza mmodzi wa abale a bambo ake. Mateyo adangofota ngati masamba a mpiru pa dothi la makande kuchigwa.

"Ngati nkotheka bwanji mundilipirire sukulu fizi yokha azakhali?" adapempha Mateyo.

"Choka apa sukulu fizinso yachiani? Ndilephere kumwa tiyi chifukwa cha sukulu fizi?" adakalipa a Natchonetsa azakhali ake a Mateyo. Adasowa mtunda wolowera Mateyo. Aliyense wa kuchikazi adalibe mphamvu. Kenaka Mateyo adaganiza msanga njira yachidule yothetsera mavuto onseŵo. Adatenga chingwe chopota cha khonje nazemba kupita kuthengo.

Atafika kuthengoko, Mateyo adayang'ana mtengo umene unali ndi nthambi yabwino. Kenaka adaupeza. Adakwera mumtengowo ndi chingwe chake chija. Adamanga mwaluso chingwe chija pa nthambi paja mbali inayo namanga khwekhwe. Mateyo atakhutira kuti

ntchito yonse yatha adaveka khosi lake mu khwekhwe muja. Asanadziponye, Mateyo adapemphera. "Ambuye, inde ndidziŵa kuti simukondwera ndi imfa yotere, koma lolani moyo uchoke mwa ine tsopano popeza ndalephera... Amen." Adapenyanso. Adaponya maso ake uku ndi uko kuti atsimikize ngati padalibe wina aliyense.

Adapempheranso.

"Ambuye, tsopano landirani moyo wanga..." Asanachite Ameni nthaŵi yomweyo adadziponya. Pamenepo chingwe chija chidayambadi kugwira ntchito yake pakhosipo. Pamene moyo wa Mateyo unkati uzifika pa mapeto, chingwe chija chidaduka. Mateyo adagwa pansi phii atakomoka.

Mayi wina yemwe ankatolera nkhuni kuthengoko adafika pamalopo koma asakudziŵa kanthu kalikonse. Nyimbo yake idali pakamwa. Nkhuni zina zili m'manja. Ankamwazamwaza maso kufuna nkhuni pa mtengopo. Nthaŵi yomwe adaponya maso kutsogolo kwake, adamuona Mateyo ali gadaa, pakamwa pali thovu lokhalokha ndipo maso ali pa mtunda.

"Chikatero ndiye n'kumati ndicho chiyani?" adafunsa mayiyo. Nthumanzi idamuomba. Adasendera pafupi kuti aone bwino. Adamzindikira kuti adali Mateyo. Nthaŵi yomweyo mayi uja adathamangira kumudzi kukauza anthu za zomwe adazionazo. Anthu ambiri adathamangira kuthengoko. Kumeneko adakampeza Mateyo ali dakhwidakhwi kuthatha pakati pamoyo ndi imfa. Msangamsanga adamumasula chingwe chija nkumutenga kuthamangira naye kuchipatala.

"Kuno ndabwera kudzatani?" adafunsa Mateyo nthaŵi yomwe adayamba kuzindikirapo zinthu. Zolankhula zake m'chipatalamo zinali zamalubwelubwe.

"Ukudwala," adayankha dotolo wina.

"Ndikudwala ineyo? Ndayamba liti? Inetu ayi sindikudwala."

"Wayamba dzulo kudwala."

"Dzulo? Dzulo lake litilo? Inu ndinu abodza eti?"

Anthu ena omwe adali pafupi ndi bedi la Mateyo

ankamva naye chisoni.

"Kodi anthu enanu mukudzatani pafupi ndi inepa?" adafunsa Mateyo, kufunsa mayi ake aang'ono Alekenianene.

"Kudzadikirira inuyo achimwene," adayankha Mayi Alekenianene.

"Aaa inu abodzanso eti?"

Ena ankafuna kusekera kumbali koma kudali kudzilimbitsa moyo kusasekako.

"Haa ndinawaona mayi ndi bambo komwe ndidapitaku," adatero Mateyo.

"Kodi mudapita kuti?" adafunsa mayiwo.

"Musandifunse! Ndipo kodi inuyo sindakufunsani kuti mukudzatani kuno? Ndabwera chifukwa chiyani kuno?" Mafunso ake adali osokonezeka. Aliyense adadziwa kuti mutu suunali bwino.

"Nanga mukudziŵa zomwe andiuza bambo atabwera?"

"Anena kuti chiyani?" adafunsa mayiwo.

"Basi andiuza zazikulu."

"Kodi akuuzani kuti chiani?" adafuna kudziŵa Mayi Alekenianene.

"Andiuza kuti ndiyenera kukhala munthu wopirira pa zovuta zonse. Ngati ndidzatero ulemerero uli ndi ine. Koma chinthu choyamba ndiyenera kuopa Mulungu." Aliyense adangoti chetee kumvera zomwe Mateyo ankalongosola.

"Ndiponso andiuza kuti, chuma chimene anthu akulimbirana kunja kunochi ine ndisakhalepo chifukwa iwo atenga themberero lochoka kwa Mulungu. Chuma cha masiye sichichedwa kutha." Pamenepo aliyense adagwedeza mutu. Ankati akamuyang'ana Mateyo pa bedipo, zinkaŵakumbutsa tsiku la maliro lija ndiye ena misozi inkayamba kubwera m'maso mwawo.

Koma chomwe chidadodometsa anthu ena pamalopo chinali chomuona nayenso Mateyo misozi ili njerengu m'maso mwake.

Patatha sabata zitatu Mateyo adachira. Koma tsiku

lotuluka m'chipatala, apolisi adatulukira.

"Kodi wachira tsopano?" adafunsa mmodzi mwa apolisi aŵiri aja.

"Inde bwana. Ali bwino tsopano kutereku akutulutsidwa lero lino," adayankha dotolo.

Nkhawa idamugwira Mateyo. Adalephera kudziŵa chomwe chinkafuna kuchitika. Koma pang'ono adakumbukira kuti munthu wodzimangirira yekha mlandu wake umafanana ndi wakupha munthu. Adadandaula Mateyo. Adaganiza kuti zoterezi zitha kumuonekera. Koma mapeto ake zinali zoonadi.

Mateyo atatuluka m'chipatala apolisi aja adamutenga ulendo naye ku polisi kukazengedwa mlandu. Uko mlandu udatsekulidwa.

"Ungatiuze chifukwa chimene umafunira kudzipha wekha?" adafunsa apolisi. Mateyo pakamwa padauma. Chonena chidamusoŵa. Kenaka adati alankhule koma ayi ndithu zosamveka.

"Ndiye kuti ineyo... ndiye kuti..."

"Talongosola zomveka! Ukuti ndiye chiyani?" adamukalipira.

"Ayi basino ndiye kuti ineyo mtima... kuŵaŵa"

"Mtima ukaŵaŵano basi koma kudzipha?"

"Ayi bwana koma kuti ineyotu bwana ndi wang'ono msinkhu. Chabwino ndidalakwa." Pamene adakhalapo Mateyo ankangonjenjemera ngati kuti adagwida nthenda ya malungo. Misozi siinkachedwa kutuluka m'maso mwa Mateyo. Nthaŵi yomweyo nyanja ya misonzi idafotsera m'maso mwake. Adafwenthera. Adasisima kenaka mibulu ya misozi idayamba kutsikira m'masaya. Adayang'ana kumbali napukuta misoziyo.

"Mateyo mlandu wako uli chimodzimodzi wa kupha munthu. Uyenera kudziŵa kuti mwamuna ayenera kukhala munthu wopirira pa mavuto osiyanasiyana pa moyo wake. Pali anthu ambiri omwe akumana ndi zoopsa pa moyo wawo. Ena tinena pano akugona pansi pa mlatho, ena akugona m'phanga ngati afisi, onseŵa ali m'mavuto. Koma chimafunika ndi kulimba mtima,"

adamufotokozera apolisi.

Mateyo adangoti zoli. Manyazi adamugwira. Fisi akagwa m'mbuna salankhula. Mateyo adatsimikiza mwambiwu.

"Mateyo uyenera kumangidwa zaka ziŵiri kuti utengerepo phunziro," adalamula. Zinalitu zovuta kwambiri m'moyo mwa Mateyo. Zimenezi zidatsimikiziratu poyera kuti ngakhale mwayi wa sukulu udalipo, zonse zidathera pomwepo. Zidaali zoonadi chifukwa nyengo ya sukulu itafika a hedimasitala aja akusukulu kwake adabwera kunyumba kwawo kwa Mateyo kudzamuona. Cholinga chawo chidali choti amtenge Mateyo akayambe sukulu. A hedimasitalawo adampezera chithandizo kuboma. Koma atafika pamudzipo adamva za nkhani yomvetsa chisoniyo. Nawonso a hedimasitala anadandaula.

A hedimasitala aja chifukwa chopwetekedwa moyo adauyatsa ulendo waku boma kuti akamuone Mateyo.

Adakampezadi kundendeko. Adamuitanitsa kuti alankhule naye. Zomwe zidachitika nzakuti Mateyo akubwera potero, maso awo adaombana. Aliyense wa iwo adagwetsa nkhope pansi. Atafika pafupi Mateyo, adanyamula mutu wake nkuŵayang'ana a hedimasitala aja. Iwonso adamuyang'ana. Kwa nthaŵi yaitali ndithu sadalankhulane china chilichonse. Ankangoyang'anitsana ngati nkhuku zotopetsana pa ndewu.

"Mateyo, ndiwo akhale mapeto ako ameneŵa?" adadandaula a hedimasitala. Konseko kunali kuthedwa nzeru. Adasoŵadi poyambira nkhani yawo.

"Chomwecho a hedi, ndicho chikonzedwe cha Mulungu," adatero Mateyo.

"Ayi Mateyo usatero kulankhula kwake. Chimenechi sichikonzedwe cha Mulungu."

"Koma nditi cha ndani?"

"Satana mdierekezi."

"Mwatero?"

"Inde mphamvu za mdierekezi zikusoŵetsa anthu mtendere. Koma..." nthaŵi yomwe ankalankhula mawuŵa a hedimasitalawo, ankangopukusa mutu wawo,

chinyontho cha misozi chili m'maso.

"Mateyo udayiŵala chinthu chimodzi chofunikira." adapitiriza a hedimasitalawo.

"Tandiuzani aphunzitsi?"

"Basi. Mwina ndidzalakwa kulankhula kwanga popeza madzi akataika saoleka."

"Ayi aphunzitsi mundiuze chifukwa mapeto a mavuto siameneŵa," adaumirira Mateyo.

"Chabwino. Chinthu chake ndi ichi; Mulungu akafuna kupereka kanthu kabwino kwa munthu kanthuko sikadza pa ufulu ayi, amayamba ndi mavuto. Ukapirira pamenepo, basi uli pabwino. Pajatu Yesu adakumana nazonso zovuta. Adayesedwa m'njira zosiyanasiyana. Adazunzidwa, adalavulidwa mate. Adakwapulidwadi koma iye adapirira. Kodi ukundiuza kuti Mulungu akadafuna kuti mwana wake asazunzike chonchija sizikadatheka?"

"Inde aphunzitsi zikadatheka."

"Chabwino. Timaona kuti mapeto ake a kuzunzika kuja, Yesu adagonjetsa imfa. Iye adakhala Mfumu ya mafumu. Ulemerero wa kumwamba ndi dziko lapansi zidamutsekulira. Lero lino adatiombola anthu tonse." Mateyo ankangogwedeza mutu. Atacheza kwa nthaŵi yaitalipo, a hedimasitala adalawira koma sadaulule kuti adafika kunyumba kwawo ncholinga chokamutenga kuti akapitirize sukulu.

Mutu 3

## Kanthu n'khama

Akuti, "masiku amathera kuchitseko". Pang'onopang'ono chaka chimodzi chidafika kumapeto. Tsopano Mateyo adayamba kuŵerenga miyezi chabe. Woyamba unadutsa. Kenaka wachiŵiri unadutsanso, wachitatu, kenaka adayamba kuŵerenga masabata, kenaka masiku.

Tsiku lina adangomva oŵayang'anira akumuitana.

Mateyo adathamanga. Uko adauzidwa nkhani ya kutha kwa ukayidi. Zaka ziŵiri idali nthaŵi yaitali. Atafika kumudzi, zinthu zambiri zidali zitasinthika. Adakapeza kuti nyumba ya makolo ake aja idagwetsedwa malinga ndi mwambo wawo. Zigayo ziŵiri zija zonse zinali zisakuyendanso, sitolo ija yomwe masiku amenewo idali yodzaza ndi katundu ija mutayereratu ndipo ku banki kulibe ngakhale wani tambala.

Zomwe zinkachitika pa nkhani ya chumacho nzakuti, chifukwa cholimbirana, wina akati nditenge ichi, wina ayi koma icho, wina ayi koma apa, mapeto ake tsopano aliyense ankadzilamulira yekha. Padalibe ndondomeko yeniyeni yoyendetsera chuma chija.

Wina ankati akatenga ndalama mu sitolomo ndiye kuti ali ndi sabata asanafike pa khomo kumwera moŵa kubala. Akati kugaitsa ufa ndiye onse adaiwaliratu kuti kunja kuno anthu amapereka ndalama kuchigayo. Kenaka zidafika muyeso wosowa ndi makobidi omwe ogulira mafuta oyendetsera zigayo. Mapeto ake adangosiya osayendetsa.

Mateyo adaona kuti chuma chonse chija sichidaŵapindulire ayi. Umphaŵi womwe adali nawo kale adaona

kuti ukalipobe. Mateyo adakhulupirira kuti chuma cha masiye sichonyadira ayi. Chinthu chofunika munthu nkudzipezera wekha chako chuma. Chuma chimatsata mwini wake. Chuma chimaterera ngati mchira wa khoswe. Adatsimikiza Mateyo. Zonsezi ankangoganiza mumtima mwake chifukwa adaopa kuti kuŵalankhula ndiye kuti akadaputa mavu pa chisa.

Patatha sabata imodzi, Mateyo adaganiza kuti kungokhala pa khomo sizimuthandiza pamene satifiketi ya J.C. yokha ali nayo. Adaganiza zoti apite ku tawuni kuti akafune ntchito. Koma vuto lidalipo tsopano ndi la ndalama za thalansipoti ndi zokadyera ku tawuniko. Adavutika mu mtima Mateyo.

'Mwina mayiŵa akhoza kukhala ndi ndalama,' adaaganiza Mateyo. Mtima wina unkamutsutsa, pamene wina unkamukankhizira kuti apemphe chithandizo kuchokera kwa mayi ake aang'ono aja. Mateyo adaona kuti mwina pakutero adzayamba kuutsapo mavuto ena. Anthu ena amaganiza movuta. Adaganiza mofulumira Mateyo.

Masiku ambiri Mateyo sankaonetsa nkhope yosangalala. Kuyenda kwake kudali kwa khumakhuma. Anthu ena omuona ankaganiza kuti mwina adakakumbukirabe umasiye, ena namaganiza kuti kapena mayi ake aang'ono aja adali kumuzunza. Choncho Mateyo adayamba kuonda tsopano. Kuyang'ana msagwada zitaloweratu, nthiti zili yoo pamtunda ngati galu wodwala chiwewe. Maganizo adamukulira Mateyo. Ankati akayang'ana nsapato zake tsopano, nazonso zidayamba kuseka kutsogolo kwake konseko kuli kung'ambika. Chitendene cha nsapatozo chitagadamuka. Ndiye poyenda ankachita kukoka ngati munthu wa thekenya. Nalonso bulangeti lidayamba kulawira. Ikakuona litsiro mvula abale, sikata mpang'ono pomwe. Kunena kwa akulu amvula zakale adatero.

"Kodi achimwene mukudwala mukuoneka kuonda chonchi?" adamufunsa mayi Alekenianene tsiku lina.

"Ayi mayi, sindikudwala nthenda ina iliyonse," adayankha Mateyo.

"Nanga kuondaku zimenezi nchabe?"

"Basi, mwina yangokhala nthaŵi yake."

"Osabisatu ngati pena pakupweteka matenda aliwonse ali ndi mankhwala ake."

"Ayi mayi musadandaule nane. Ine ndili bwinobwino."

Mateyo adalephera kuulula chomwe chinkamvuta mumtima mwake. Maganizo ofuna kupita ku tawuni adakulirakulira. Kenaka Mateyo adaona kuti manyazi sapindula. Tsiku lina adakhala nawo pansi mayi akewo.

"Koma mayi ine ndikuganiza zopita ku tawuni kukafuna ntchito?"

"Kutawuni?"

"Inde mayi."

"Hmm. Koma ukuganiza kuti ntchito ukayipeza?"

"Izo sindingathe kudziŵa mayi popeza zonse chimakhala chikonzero cha Mulungu."

"Apo nzoonadi. Ngati Mulungu adalemba kuti udzayamba ntchito sipadzafafanizika mwana wanga. Chifukwa mwina anthufe timaiŵala kuti pologalamu yonse ya munthu ndi ya Chauta. Mwina tikhoza kuona kuti zimene ife tikuganiza kuti tichite nthaŵi yakutiyakuti mwina zimalephereka. Ine sindingatsutse maganizo ako. Kodi tsopano ndalama za thalansipoti zilipo? Nanga uko kutawuni ukafikira kuti popeza kulibe wina aliyense wachibale?"

Mafunso aŵiriŵa adamuzunza Mateyo. Makamaka funso lomwe lidamusoŵetsa mtendere ndilo la malo okafikira m'tawunimo. Pamenepo adakhala kaye phee. Kenaka adayankha. "Mayi musadandaule ndi zinthu zambiri. Ine ndi munthu wamwamuna. Pamene pali chabwino payenera kupezeka zovuta zina. Mtendere siubwera wokha kulikonse. Pajatu akuti, sikadza kokha kaopa kulaula."

"Indedi achimwene. Koma vuto mwina ndi la thalansipoti chifukwa ku tawuni ndikutali." Anadandaula mayiwo.

"Ayi mayi, basi izo zatha musadandaule. Ndiona

chochita. Ndakula ndatha. Zovuta za dziko lapansi lino zidabwerera anthu osati nyama zakuthengo."

Atatha kukambirana Mateyo adachoka kupita ku mphala kwake. Adayala mphasa m'nyumbamo nagona pamenepo kudya mutu.

Adazama Mateyo m'nyanja ya maganizo pamenepo. Mapeto ake adadziŵa choyenera kuchita.

Akuti mwamuna sauzidwa amaopa kunamizidwa. Mateyo adaona kuti kungokhala zala lende, kapena kumangodzipha ndi madandaulo mumtima zonsezo zidalibe phindu lake. Kukomera kwake idali nthaŵi yolima. Anthu ofuna anyamata aganyu adalipo ambiri. Ndiye Mateyo adaona kuti samu yowonjezera yasiyana ndi yochotsera. Kuyambira tsiku limenelo Mateyo adayamba kumakalimitsa ganyu. Akapita kumunda kwawo mmaŵa ndiye madzulo ake apita kukalimitsa ganyu. Kulima kwake kudali kodzipha. Chauta apatsa munthu wolimbika. Mwambiwu Mateyo adaugwiritsadi ntchito. Ndiye pa tsiku amalimitsa 12 tambala nthaŵi zina 15 tambala.

Ankati akapeza mwayi wa kontalakiti ndiye kuti pamenepo ankakokera moti pakutha pa malowo ankalandira kwacha mwinanso kwacha ndi ana ake. Ayi pamenepo mwini wakeyo ankadziŵa kuti mphongoyi yachita chamuna. Padali zinthu zambiri zimene Mateyo ankachita kuti apeze ndalama msanga. Nthaŵi zina ankagula nzimbe ku madimba a anthu. Iyeyo ankakagulitsa ku msika pa mtengo wokwerapo. Ngati agula nzimbe za 50t ndiye kuti ankakokera mwina ankapezanso phindu la 50t.

Ndalama zitakwana 10 kwacha, Mateyo adaganizanso kuti azigula nkhuku kapena nyama ya ng'ombe kaya ya nkhumba kuti aziphika kanyenya. Maganizoŵa sadasinthe chifukwa iye cholinga chake chidali choti apeze ndalama zochuluka mwina 20 kwacha kapena 30 kwacha kuti zinazo azikagulira zakudya m'tawuni. Mateyo ankakagulitsa kanyenya uja kumalo amoŵa kapena apo ayi ku siteshoni ya sitima. Udaalitu ulendo wautalipo kuchoka kumudzi kwawo kukafika ku siteshoniko.



BOSTON UNIVERSITY
1 1719 01826 7866

Komabe Mateyo ankayesetsa.

Tsiku lina Mateyo lidamuonekera tsoka lina lomwe lidali chidindo chosaiŵalika pa moyo wake. Atafika ku siteshoni ya sitima, mbale yakanyenya ili m'dzanja lake monga mwachizolowezi, ankati sitima ikafika pa siteshonipo Mateyo ankaloŵa ndi kanyenyayo. Tsiku limenelo Mateyo adachita chimodzimodzi. Sitima itafika Mateyo adakwera m'sitimamo.

"Yesi makasitomala! Kanyenya! Kanyenya! Kanyenya! kupeza kanyenya pano," adanenerera Mateyo.

"Tabwera naye pano mnyamata!" mayi wina adayitana.

Mateyu adapita pamenepo.

"Mayi, mukuona bwanji? Ndimatengera makasitomala anga kanyenya wa fesiti gredi."

"Ndiye mukuchita bwanjibwanji?" adafunsa mayi.

"Pang'ono chabe mayi: malo aŵa, 10 tambala; enaŵa 15 tambala, tsopano ponse apa 25 tambala."

"Tandipatseni mmodzi wa 15 tambalayo," adatero mayiyo.

"Eee! mnyamata wakanyenya, ubweretse kuno ukathana nawo amenewo!" bambo wina adaitanitsa.

"Inde bambo ndikubwera osadandaula sitifuna kukhumudwitsa makasitomala!" adayankha Mateyo.

Indedi, Mateyo adali wotanganidwa kotero kuti monse sitima imayamba kunyamuka sadazindikire kanthu. Anthuwo sadathe kumuuza chifukwa adakhala akuona anyamata ambiri akanyenya akukwera sitima nkukatsikira siteshoni ina.

Pepani, Mateyo atazindikira kuti sitima idayamba kuyenda, adadzidzimuka nayamba kuthamanga kuti akatsike. Nthaŵi imeneyo Mateyo adaiŵalilatu zoti anthu ena atatu musitimamo adatenga kanyenya koma osalipira. Mateyo atafika pakhomo adalumpha ndaa, ali pansi phii! Kanyenya uja yense pansi mbwee. Mwayi wake iyeyo sadavulale chifukwa adafulumira kuchotsa mwendo msanga mu njanje, pang'onong'ono ikadamuponda.

"Iiii, ngozi!" adakuwa anthu ena. Musitimamo ambiri adatulutsa mitu m'mazenera kuti aone zidachitikazo. Mateyo adafulumira kudzuka nayamba kudzisansa fumbi. Ena m'sitimamo ankaseka, koma ena ayi ankamumvera chisoni. Moyo wa Mateyo udadzala ndi mkwiyo.

Kuona kuti malonda ake awonongeka, adadandaula kwina akungopukusa mutu. Sitima itapita adayamba kutola kanyenya uja ngakhale adadziŵa kuti sakadagulitsanso. Akutola kanyenya uja adamva munthu wina akumuitana. Mateyo adawelamuka. Adaponya maso ake kutsogolo.

"Ndiwe Selina!" adalankhula Mateyo mwamanyazi.

"Ndiwenso kodi Mateyo!" Selina naye adakuwa.

Selina Kataye adali msungwana amene ankaphunzira naye limodzi uja ku Sekondale Sukulu kuyambira fomu wani mpaka fomu fili. Mateyo msungwanayo ankamufuna kuti akhale bwenzi lake kusukulu. Adamukonda chifukwa chakukongola. Kadalidi kamsungwana kamene Chauta adaonetsadi luso la chilengedwe. Kadali kakafupi bwino, khungu lake losalala, koyera, tsitsi lake la mzindo. Kuyang'ana timaso take kuyera ngati tankhunda, mano ali mbee kuyera ngati mpunga wa faya. Ankati akamamwetulira, omuonawo thupi lonse linkamveka kuzizira ngati aponda mu ufa.

Chimenecho chidali chilengedwe chake.

Nayenso Selina chikondi adali nacho kwa Mateyo. Onseŵa ankakondana koma kuti mwina Mateyo ankangouma pakamwa kuti nkhani ya chikondi chawo ayivumbulutse. Mateyo naye masiku amenewo adali ka nyamata kooneka bwino, kuyera kali mbee.

Ndiye ndi nzeru zija za m'kalasi, Selina ankangotsinzinira kuti kamnyamata koma kameneka, ati kamnyamata kodyetsa wani.

M'kalasimo, Selina ankati samu ikamuvuta pena pake ankafika pakhundu pa Mateyo basi, nkumaphunzitsana.

"Iwe Mateyo ndipatali eti?" ati kuyamika, Selina ankatero, timaso tili mbee ngati wopanda magazi.

"Choka apa, paja ndiwe wokonda za chibwana eti?"



BOSTON UNIVERSITY
1719 01826 7866

Mateyonso ankalankhula kukhosi kuli myaa ngati wameza batala.

"Chibwana ngati koma kuti..." Mwina Selinayo ankaiwala kuti ali m'kalasi. Kulankhula kwake nthaŵi zina ankalankhula mokweza mawu.

"Shii. Undigwiritsa chibalo iwe," ankawopseza Mateyo.

"Iii basi ndaleka." Akatero, ankangomwetulirana.

"Kodi lero lino n'kutulo kumuona Selina?" Adadzifunsa Mateyo. Zimenezi zidamukumbutsa zambiri za ku sukulu. Nkhope ya Mateyo idaonetsa manyazi.

"Tsopano Mateyo ukuchita chiyani pamenepa?" adafunsa Selina. Mateyo sadathe kuyankha funsolo.

Tsiku limenelo Selina adatchena bwino. Tsitsi lake la mzindo lija tsiku limenelo adatiwa mwamakono. Adavala siketi yofiira ndi bulauzi ya gileyi m'chiunomu atamanga lamba wamkulu wakuda. Kuphazi nako kudali nsapato yodula, mtundu wake woyera. Ena omuona ankangoganiza kuti mwina adangotsika kumene ndege sabata imodzi yapitayo kuchokera ku Mangalande.

Mateyo adavala thalauza long'ambikang'ambika. M'maondo mwa thalauzamo mudali mosokedwa ndi ulusi pamanja ndipo ulusi wake wosiyana mtundu ndi thalauzalo. Malaya ake adali ong'ambikanso. Nsapato zoseka kutsogolo. Ndiye ndi kugwa pansi kuja ngakhale adayesetsa kudzisansa fumbi, adaonekabe mbuu kutuwa, m'manja mwake muli mafuta a kanyenya noninoni.

"Selina! Ndiwedi Selina iwe!" adatero Mateyo mmalo moyankha funso lija. Kulankhula kwake kosasangalala. Adapitiriza mmalo mofuna kudzisangalatsa. "Tsopano uli kuti kaya nditi ukugwira ntchito kuti?" adafunsa Mateyo.

"Ndili ku Yunivesite tsopano, ku Chanco. Ndikutenga Genelo Digiri," adatero. Adanyowa ndi manyazi Mateyo.

"Nanga Suzeni Dzala ndi Chisombezi Kaduka onse ali kuti?" Mateyo adapitiriza kufunsa.

"Suzeni ali ku koleji ya ntchito zamanja. Chisombezi ndili naye limodzi ku Chanco koma iye akutenga za ma

sayansezi *(Sciences)* pajatu iye uja amakonda Fizikisi *(Physics)* ndi Bioloje *(Biology)*," adalongosola Selina.

Mtima wa Mateyo udayaka moto. Adasilira Mateyo. Misozi inkafuna kubwera m'maso mwake koma adadzilimbitsa.

"Nanga iwe uli kuti tsopano?" adaliponya funso Selina. Lidali funso lovuta kwambiri kuliyankha kumbali ya Mateyo, mmalo mwake adangomuyang'ana Selinayo kunkhope kwa nthaŵi yaitali. Kunena zoona funsolo Mateyo sadayankhe.

"Kodi Saduki Kausipa ali kuti tsopano?" Mateyo adaphiphiritsa. Selina adagwa nayo mseko. Poyamba Mateyo adaganiza kuti ankamuseka iye koma kenaka adadzazindikira msanga kuti ankaseka Sadukiyo. Saduki adaali mnyamata amene ankamuseka kaŵirikaŵiri m'kalasi. Adali kuoneka wopusirapo, wofatsa ndipo pamfuno pake mamina sankachoka ayi. Dzina lomusinjirira ankamutchula kuti Kamamina. Dzina limeneli Saduki ankapsa nalo mtima ndiye onse m'kalasimo ankakuwa kuti 'Kamaminaaa!' Akatero Saduki ankaipidwa kwambiri pafupifupi kufuna kuchita ndewu m'kalasi. Makamaka Saduki ndi Selinayo adali adani chifukwa choti Selina adali waphwete kwambiri.

Tsiku lina Selina adalandirapo pama kuchokera kwa Saduki atapsa mtima. Atangomuomba pamalo ndiye kalasi lonse lidagwa m'chiphokoso kumupokosera Saduki. Kunena kophera mphongo, Saduki ankasoŵadi mtendere. Selina atasiya kusekako adayankha.

"A Saduki tsopano ndi aphunzitsi a ku pulaimale." Koma nkhope ya Selina inkasonyezabe kuti ankafuna kuseka.

"Koma zinthu zimasintha eti? A Saduki lero ndi aphunzitsi," adatero Mateyo. Selina adasekanso.

"Komatu ine pachipanda zovuta zina bwenzi tiri limodzi ku Chanco kapena ku Poly," anadandaula Mateyo. Selina adasintha nkhope.

"Iwe udali wosakaikitsa ayi. Koma usadandaule popeza mapeto adziko samenewa. China chilichonse

chitha kuchitika ndipo zoterezi nkumadzaimba ngati nthano," adamulimbitsa Selina.

"Zimenezi ndi zosadziŵika Selina."

"Mateyo, kuno n'kunja khala chete. Mulungu akonza njira ina. Mulungu adzakutsogolera," adatero Selina.

Mateyo ndi Selina adakambirana nkhani zambiri. Kenaka Selina adayamba kufotokoza za moyo wa ku yunivesite. Mateyo adaonadi kuti moyo wa ku yunivesite ndi wabwino kwambiri. Adasirira Mateyo. Nthaŵi yomwe Selina ankagundika kulakatula nkhaniyo, Mateyo adangoti pakamwa pululu.

Nkhani ili mkati, Selina adachita ngati wadzidzimutsidwa pang'ono. Potero pankabwera kamnyamata kena kooneka bwino ndithu kakatalipo, kakuda komukhala, magalasi ali kumaso, mavalidwe ake abwino, nsapato ya kuphanzi kwake yowopsezanso. Indedi Selina adachita jenkha pang'ono, chimwemwe chidayamba kale kusefukira pa milomo yake.

Nthaŵi yomwe mnyamata uja amafika pafupi Selina adamuuza Mateyo, "Ameneyu ndili naye limodzi ku Chanco. Kuteleku chaka chino ndi chomaliza chake kuti atenge digiri. Koma ..." Sadathe kupitiriza Selina popeza mnyamatayo nkuti atafika kale.

"Welokhamu mayi diala!" adatero Selina mu Chingerezi.

"Yesi mayi diala. Thankiyu!" adayankha mnyamatayo. Selina adamgwira pamkono napsopsona dzanja lake, ati kutanthauza moyo wa chizungu. Zonsezi Mateyo ankangoyang'ana. 'Chauta apatsa mosiyana,' Mateyo adatero mumtima mwake.

"Iwe Machona, uyu dzina lake ndi Mateyo Taonana, ndidali naye limodzi ku sekondale sukulu koma chifukwa cha zovuta zina adasiyira mu fomu fili.

"Tsopano Mateyo, uyu ndi mnzanga kaya nditi amene adzakhale mwamuna wanga mtsogolomo."

Atakhala pang'ono Selina ndi Machona adalawira natengana. Ankayenda atagwirana manja, ati kutanthauza chikondi chaponda apa nane n'pondepo, chikondi cha

chizungu. Mateyo adaonadi anzakewo ngati kuti ndi anthu ophunzira. Pamenepo Mateyo adangoima phee, kumangoŵayang'ana akupita poteropo, mmenemo nyanja ya misozi ikudzala m'maso mwake. Adasisima.

Mutu 4

## Wapsa wa ku Tawuni

Zonse za ulendo wa ku tawuni zidakonzedwa. Mateyo adakonza kuti adzanyamuka tsiku Loweruka.

Mayi Alekenianene adatenga chimanga m'nkhokwe nkumugayitsira mgayiwa kuti akhale kamba wa paulendo. Adampatsanso nyemba, khobwe ndi nzama kuti azikadya. Mateyo adasangalala. Nthaŵi imeneyo m'thumba muli 30 kwacha ndi matambala fifite. Komabe nthumanzi inkamuomba akaganizira za kutawuni.

Mateyo podziŵa kuti idali nthaŵi yoyamba kupita m'tawuni, ndiponso kudziko kopanda mbale aliyense, mtima wake unkamuthaŵathaŵa.

Loŵeruka litakwana, Alekenianene adamfunira mafuno abwino Mateyo. Adamutsogoza ndi mapemphero. Adamulimbitsa mtima. Alekenianene sadayiwale kumuchenjeza za moyo wa m'tawuni. Adamuchenjeza za magalimoto mumsewu. Adamuuzanso ubwino wokakhala ndi anzake kumeneko. Mateyo zonse ankangoziika pansi pa mtima wake.

Tsiku limeneli mayi akewo pamodzi ndi anzake ocheza nawo adamperekeza ku siteshoni ya sitima.

Kuja sitima siidachedwe tsiku limenelo. Atangodula chipaso nthaŵi pang'ono sitima nayo idatulukira. Mtima wake udayamba kugunda kwambiri maka podziŵa kuti tsopano adzalekana ndi anzake aja pamodzi ndi mayi ake. Mateyo adadziona yekha ngati mwana uja wolowerera. 'Ndikafikira kuti?' Funso limeneli ndilomwe linkamuvuta kwambiri Mateyo. Maso ake adaoneka kufiira, kenaka misozi idachita njerengu m'maso mwake.

Sitima itaima, Mateyo ndi anthu ena adakwera. Mwamwaŵi Mateyo adapeza mpando ndipo adakhala. Nthaŵi pang'ono ulendo udayambika. Adatulutsa mutu pawindo Mateyo kuti alawirane ndi mayi ndi anzake adamuperekeza aja.

"Kafikeni bwino achimwene!" adatero a Alekenianene mmenemo manja ali kupekupe m'mwamba.

"Tsalani bwino mayi, tsala bwino Joni, tsala bwino Tebulo, tidzaonana...." Indedi, udali ulendo wabwino.

Chapambali pakepa m'sitimamo padakhala mnyamata wina yemwe ankaŵerenga nyuzipepala. Mateyo adachita chidwi ndi nyuziyo.

Chinthu choyamba Mateyo adampatsa moni mnyamatayo koma molimba mtima chifukwa maonekedwe a mnyamatayo ankaoneka ngati munthu wosafuna kuzolowereka.

"Moni achimwene?" adatero Mateyo.

"Zikomo." Basi kuvomera kwake kudali komweko kenaka nkumapitiriza kuŵerenga.

"Ulendowu mukupita ku tawuni?" adafunsabe Mateyo.

"Inde ndikupita mtawuni." Adayankha mnyamatayo nthaŵi yomweyo basi, nkumapitiriza kuŵerenga osamuyang'ananso.

"Mumagwira ntchito kampani iti?" adafunsa Mateyo.

Mnyamata uja anadayankhe funsolo adamuyang'ana kaye Mateyo ku nkhope. Maso awo adawombana.

"Ufuna kudziŵa zambiri za ine eti?" adafunsa mnyamatayo.

"Inde, nanga sikuti ulendo ufupike basi?" adayankha Mateyo. Pamenepo adaonetsa kuchenjeradi.

Mnyamata uja adapitiriza kufutukula nyuzi pepala ija. Adaonetsa kusalabadira naye konse.

"Umadziŵa kuŵerenga?" adamufunsa mnyamatayo mmalo moyakha funso lija.

"Inde ndimayesera bwana," adayankha Mateyo modzichepetsa. Pokhapo Mateyo adadziŵadi kuti kudzichepe-

tsa pa maso pa anzako kaya akuluakulu ndi njira yokhayo yothandiza. Yesu naye ankadzichepetsa... 'Yesu adatsuka mapazi a ophunzira ake... konseko kudali kudzichepetsa...' adaganiza Mateyo.

"Iweyo uziŵerenga magaziniyi." Mnyamata uja adatulutsa magazini kuchokera m'chikwama.

Atalandira magaziniyo, Mateyo adafunsa.

"Akusindikiza kuti magazini imeneyi?"

"Kutawuni komwe tikupitaku."

Mnyamata uja adayamba kumasuka chifukwa nthaŵi yomwe amayankha funsoli amamwetulira.

"Paja umafuna kudziŵa komwe ine ndimagwira ntchito eti?" adatero mnyamatayo.

"Inde bwana," adayankha Mateyo.

"Ndimagwira ntchito ku Lokoma Enterpulaizi. Ntchito yanga ndi ya akauntanti – yolongosola za ndalama," adalongosola mnyamata. Kenaka adaonjezera.

"Dzina langa ndi Aonenji Chitsulo, ndachokera ku Dzandula Boma."

Mateyo ankangogwedeza mutu. Iyenso Mateyo adayamba kumasuka. "Ndakondwera kukudziŵani. Ine dzina langa ndi Mateyo Taonana. Kwathu pakadali pano ndi konkuno ku Mphichi. Ndikupita m'tawuni kukafuna ntchito. Sukulu ndidasiyira fomu fili basi," adafotokoza Mateyo.

Aonenji adamuyang'ana Mateyo.

"Udalekera sukulu fomu fili chifukwa chiyani?" adafunsa Aonenji.

"Zovuta ndi zambiri pa dziko lapansi lino achimwene. Makolo anga adamwalira pangozi ya galimoto. Basi, tsogolo langa lidathera pomwepo," adatero Mateyo.

"Pepa ambwana. Koma tsogolo lako sikuti lidathera pomwepo ayi. Ndiye kuti padalibe mbale woti akadakuthandiza?"

"Ayi padalibe ndipo kuti ndilongosole nkhani yonse ndiye kuti mpaka tikafika ku tawuni. Koma basi... chabwino ndiye kuti ntchito zikupezeka m'tawunimu?" adaphiphiritsa Mateyo.

BOSTON UNIVERSITY
1 1719 01826 7866

"Nkhani ya ntchito ndiyovuta kulongosola kwake chifukwa nthaŵi zina imayendera mwaŵi wa munthu," adamuuza Mateyo.

"Apa mwanenadi bwino. Ayi ndikaonera komweko."

"Komansotu pamakhala mwaŵi wophunzira ntchito zina ndi zina ku malo osiyanasiyana. Monga momwe ukuionera magaziniyi. Pali anyamata ena amakaphunzira za kasindikizidwe ka mabuku, manyuzipepala ndi zina ku malo ophunzirirako ntchito zamanja."

"Musandiuze achimwene, monga ndi zoona?" adaonetsa kudabwa Mateyo. Nkhaniyo idamugwira mtima.

"Ine maganizo anga adali ofuna kudzakhala owulutsa mawu pa wailesi, ndiye poti zimene munthu umafuna nthaŵi zina sichimakhala chikonzekero cha Mulungu."

"Apodi wanena zoona. Komabe osada nkhawa kopitirira mwina mwaŵi wa ntchito ukapezeka. Zikakhala za makozi a ntchito zina ndi zina monga ngati zija ndinanena amachita kulemba munyuzi ngati iyi ndiye anthu amalembera. Akadzakhoza intavyu basi amakayamba."

"Ndi zabwino eti," adavomereza Mateyo kutsimikiza kuti nkhaniyo idamugwiradi mtima.

Chifukwa chochuluka nkhani ulendo udaoneka ngati waufupi. Kudali kovuta kuzindikira kuti tsopano adafika m'tawuni.

"Tafika mnyamata m'tawuni. Kodi okuchingamira alipo?" adafunsa Aonenji.

"Ayi palibe ndiponso sindidziŵa aliyense m'tawuni muno," adayankha Mateyo.

"Tsopano uchita bwanji pamenepa?" Mateyo sadayankhe msanga. Adamuyang'ana Aonenji. Maso awo adawombana. Kenaka Mateyo adagwetsa nkhope yake pansi.

"Basi, Chauta andithandiza. Mbalame zakuthengo ndi nyama zimakhala ndi moyo zaka zochuluka koma sizigwira ntchito ina iliyonse, ndiye Mulungu aleke bwanji kuthandiza ine? Musadandaule achimwene moyo umazunza nthaŵi zina."

Aonenji adachita naye chidwi Mateyo, adadziŵa kuti

Mateyo sadali mwana ayi koma nzeru zake zidali zakuthwa.

Sitima ikuyandikira pa siteshoni tsopano, chigulu cha anthu chidali yakaliyakali pamenepo.

"Akumangoni atulukira! Tidye mbewa!" ena achipongwe ankakuwa chomwecho. "Mnyamata uchenjere ndi anthu akuba mtawuni muno ngati uli ndi katundu," adamuchenjeza Aonenji mnzakeyo.

"Pamenepo mwachita bwino achimwene," adayamikira Mateyo.

Sitima itaima onse aŵiri adatsika, Mateyo adanyamula sutikesi ndi kathumbanso kena komwe adaikamo ndiwo.

"Bwanji thalansipoti iliko, muyifuna?" anyamata ena amagalimoto ochititsa hayala ankatero pa siteshonipo. Mateyo ankangoti maso naponya uku, kenaka uko kuli kusoŵa koloŵera.

Mnzake uja Aonenji adalawira kuthamangira kukakwera basi. Nthaŵi yomweyo Mateyo adakumbukira msanga za moyo wa m̂tawuni. Adanyamula katundu wake uja kupita panyumba ina yogona anthu apaulendo pa siteshoni pomwepo nkukakhala pamenepo.

Usiku umenewo Mateyo sadatione tulo chifukwa cha maganizo.

"Kodi adzandilola kugona malo ano kwa masiku ochuluka?" ankadandaula Mateyo. Ndiye pogonapo ngakhale anthu ena apaulendo ankakamba nkhani zochuluka ncholinga chofuna kuchepetsa usiku, zonsezo Mateyo ankaziona zopanda ntchito. Iye kukhala kwake adangoti khumaa, mutu wake atatsamiritsa pa kathumba kake kaufa. Pamenepo ankati akati gunthii, naliza pang'ono mkonono, basi kenaka uyo wadzidzimuka. Kukhala kwake kudali ngati kwa mbidzi yopumula pamthunzi pofuna kuphwetsa nkhuto.

"Achimwene kumalankhula mkamwa muchita ndele," mkulu wina adatero.

"Inde wawa zonsezi ndikumva," adayankha choncho Mateyo.

"Chifukwa tikuona kutitu mwafatsa ndikuganiza?" adapitiriza mkuluyo.

"Ayi basi kungofatsa wawa," adatero. Indedi kuti mpake akuluwo kumufunsa Mateyo. Aliyense pamenepo ankaseka. Ankati wina akaiphulitsa yake nkhani ndiye kuti nthaŵi imeneyo winanso ali mkati kuiphika ina. Chifukwa chankhani zaozi, ndiye monse atambala ankalira kudali kovuta kuzindikira kulira kwa atambalako, kupatulapo Mateyo basi.

Mmaŵa kutacha, aliyense adayalula choyala chake nkupinda bwinobwino. Ena ankathamangira kodula matikiti. Mateyo nthaŵi imeneyo adangokhala chatsonga phee. Anthu ena chifukwa chomuona kuti zaulendo sankavunduka nazo, ankaganiza kuti mwina ndi mmodzi mwa akapsala, akamatule.

"Kodi achimwene simukadula tikiti yanu?" adafunsa mkulu wina.

"Ndikadulabe wawa," adayankha mochenjera Mateyo.

"Nthaŵitu ndiye yatha," adapitiriza mkuluyo.

"Ayi bambo musadandaule nane. Aliyense pano akuyendera pologalamu yake." Pamenepo Mateyo adaonetsadi kuyankha mwachamuna. Mkulu uja adangoti kwakwalala, kuchokapo.

Mmene dzuŵa linkatuluka, pa malo ogona anthu apaulendo padalibe aliyense. Mateyo adatsala yekha. Poganiza kuti mwina anthu ena ogwira ntchito pomwepo adzamfunsa mafunso ambiri, iyenso Mateyo adachokapo natenga katundu wake.

Mateyo posafuna kudzivutitsa kwambiri ngati makobidi adalibe, adapita malo ena m'tawuni kukafuna nyumba ya lenti. Mwamwaŵi sadavutike kwambiri nkufunafuna, adaipeza. Pamenepo mtima wake udazizira pang'ono.

Mutu 5

## Linda madzi apite ndiye uziti ndadala

Mateyo adayesetsa kufunafuna ntchito m'tawuni. Tsopano mwezi unkapita kumapeto. Ufa ndi makobidi zonse zidayamba kutha. Anadandaula. Mateyo ankalemba makalata angapo ofunsa ntchito tsiku ndi tsiku. Iyenso sankakhala pansi. Masana sankadya chilichonse ndipo ankangomwa madzi basi. Masiku ena ankati akachoka m'tawuni, ankapita ku Lebala Ofesi kuti mwina mwaŵi wa ntchito akadaupeza kumeneko.

Mateyo ankati akapita ku Lebala Ofesi, kumeneko ndiye ankaiŵala mavuto ambiri. Kudali kuchitika maseŵero osiyanasiyana monga: bawo, drafuti, nokonoko, thulufu, chesi ndi ena ambiri.

Kuyambira akali kusekondale sukulu, maseŵero a chesi, Mateyo ndiye kudali kudya kwake. Ankaŵakonda maseŵeroŵa. Ndiye ankati akaigwira chesi kuloŵa kwa dzuŵa sikunkaoneka kutalika.

Madzulo akabwera kunyumba ndipo akatha kudya mgonero, ankagona pa mkeka m'nyumba, nkuyamba kumakumbukira zomwe zidamuchitikira masanawo. Nthaŵi zina ankaseka yekha m'nyumbamo ngati munthu wamisala...

"Ukufuna chiyani mnyamata?" adafunsa ndi mawu aukali mlonda wa pakhomo pa mpanda wa kampani.

"Ndikufuna kukaonana ndi bwana wolemba anthu ntchito," adayankha Mateyo ndi mawu wa munthu wolimba mtima.

"Ayi, pano palibe ntchito," mlonda adakana.

"Mwadziŵa bwanji kuti palibe ntchito popeza

wolemba anthu ntchito ali kuofesi?"

"Basi nthaŵi zonse akafuna kulemba anthu ntchito choyamba amandiuza ineyo pano."

"Bwanji mundilole kuti ndikaonane nawo ndekha?"

"Ayi ndati palibe ntchito. Bwanji makani?" adayamba kukalipa.

"Kodi bambo pali chifukwa chanji choti akuuzeni inu za ntchito bwanawo?" adachita makani Mateyo.

"Imeneyo ndiyo ntchito yanga pano," adayankha tsinya lili thee, pamphumi. Nthaŵi zina Mateyo zoterezi zidafika pomugwira thupi. Ankati akapezana ndi mlonda wotere iye ankafuna zosereula naye.

"Pepa mnyamata, pano ntchito mwina ukadabwera dzulo akadakulemba."

"Zimenezi mwadziŵa bwanji bwana?"

"Basi andiuza kuti wina aliyense asalowenso ku mpandaku pa nkhani yantchito."

"Mukunena zoona?"

"Inde ndizoona."

"Ngati palibe ntchito nanga inu mukupezeka bwanji pamenepa?" Pamenepo mlondayo sankayankha. Akatero Mateyo amangoyambapo ulendo kumapita. Koma malo ena Mateyo ankalowa nkukalankhula nawo bwana...

'Zoonadi nkofunika kuti munthu uziyenda kuti uone agalu amichombo,' adaganiza Mateyo mumtima mwake. Chifukwa chotopa nkuyenda m'tawuni, Mateyo adaganiza zoti mwina angobwerera kumudzi.

Tsiku lina Mateyo adadzuka ali wotopa kwambiri. Maganizo oti akadapita ku tawuni ncholinga chofuna ntchito adalibe. Dzuŵa litakwera, maganizo ena adamufikira Mateyo kuti apitebe ku Lebala Ofesi kukangozonda. Adauyatsa ulendo satifiketi yake kudzanja. Atakafika adapeza anthu ali m'magulumagulu monga mwa nthaŵi zonse. Iye adapita pomwe ankayenda chesi. Tsiku limenelo Mateyo sadafune konse kuyenda nawo. Ngakhale anthu ena ankamuumiriza kuti ayende nawo, Mateyo adamenyetsa nkhwangwa pa mwala. Kenaka Mateyo adaona anthu akuthamangira ku ofesi. Iyenso



BOSTON UNIVERSITY
1719 01826 7866

adathamangira nawo kumeneko.

"Tikufuna munthu wa satifiketi ya J.C. ndipo wokhoza masamu!" Mateyo adamva ofesala wa za antchito akulengeza. Nthaŵi yomweyo Mateyo adafika pafupi ndi satifiketi yake. Adampatsa ofesalayo ndipo adamuuza kuti abayembekezera potero.

Adatenga anthu angapo kuti akachite mayeso kumeneko.

"Inu mupite ku kampani ya Simbani Zatha, akufunako mesinjala mmodzi," adaŵauza ofesalayo.

Mateyo adasangalaladi. Adadziŵa kuti chomwe wapatsa Chauta nchomwecho. Nthaŵi zonse kalikonse kamakhala ndi chiyambi. Mateyo adadzifanizira ndi munthu amene amafuna kukwera pa tsindwi (padenga) la nyumba. Munthuyo choyamba amafunafuna makwerero amene amakhala ndi masitepu angapo. Akaŵapeza amaonetsetsa kuti waŵaika malo oyenera ndipo akhazikika bwino. Atakhutitsidwa munthuyo amayamba kukwera sitepu imodziimodzi mpaka amakafika pa tsindwipo. Nkosatheka konse munthu kungofikira sitepu ya mapeto, basi ali pa tsindwi asadayambepo waponda sitepu yoyamba. Uku kudali kuganiza kwake Mateyo.

"Ndimwaŵi wapadera umenewu," adatsimikiza Mateyo mumtima mwake. Adadziŵa kuti malo amenewo akamutenga.

Zidali zoona chifukwa atafika ku Simbani Zatha Kampani, nalemba mayeso, bwana adadziŵadi kuti Mateyo adali ndi nzeru koma kuti zinthu zidangoona kumuvuta. Mayeso amene adalembawo, Mateyo adakhoza nainte-faifi kwa wani handedi. Omutsatira wake nkudzapeza sikisite. Apo zidaonekeratu poyera kuti Mateyo adalembedwapo ntchito.

"A Mateyo Taonana mwalembedwa ntchito pano ndiye monga mukudziŵa ntchito yanu ndi yokonza mu ofesi kaya titi 'ofesi boyi' pa chingerezi ndikutumikira (Mesinjala)," adamuuza Mateyo bwana wamkulu pa kampanipo, (Jenolo Manijala). Mateyo adasangalala.

"Zikomo bwana," adathokoza Mateyo, nkhongono zili

njenjenje.

"Ndiye bwana wako ndi bambo a Choyipira Bwezani. Pamalo pano amadziŵika kwambiri ndi dzina loti a Bwezani. Mwamva?"

"Inde bwana."

Atalongosoledwa zonse Mateyo adamutenga bwana wamkuluyo kukamusiya ku ofesi ya a Bwezani. Mateyo chimwemwe chidali tsaya podziŵa kuti tsopano ntchito adaipeza.

"Kwanu nkuti?" adafunsa a Bwezani, tsinya lili theee pa mphumi pawo. Mateyo adayankha momangika thupi.

"Kwa... kwathu ndi ku Mpichi bwa...bwana," adajejema Mateyo ngati munthu wachibwibwi..

"Sukulu udalekeza kalasi yanji?" adafunsa lina funso.

"Fomu fili bwana."

"Fomu fili ndiye kuloŵa ntchito imeneyi?"

"Chomwecho bwana, nanga nkutani."

"Anzathu ophunzira chomwechi mungakhale boyi? Inu sindiye ofunika muli maofisala?" adanyoza a Bwezani.

Mateyo adalephera kuyankha funsolo. Adangowayang'ana kumaso. Nthaŵi yomweyo a Bwezani adakoka 'fani' pafupi, basi, nkuiyambitsa kuyenda ngati kuti kunja kunkatentha, koma ayi onsewo ali matama.

"Chabwino. Ine ndiye mkulu amene ndimayang'anira 'Dipatimenti' yonse ino. Kuno uzikhala ndi ine monga wauzidwa kale. Zonse zimene uzipanga ndizikuuza ndi ine, wamva?" Ankalankhula chomwecho, bolopointi akungokandira kumutu ngati kuti kunkayabwa.

"Inde bwana. Ine ndabwera kudzagwira ntchitoyo basi," adayankha Mateyo. Atatha kukambirana, a Bwezani adamuuza kuti tsopano akhoza kuyamba ntchito.

Patatha masiku angapo, Mateyo adayamba kuzolowerapo pa malopo. Adayambanso kuzolowerana ndi anthu ena ogwira nawo ntchito. Ena ankamulongosolera za ubwino wa pamalopo, ena zoipa zake. Mateyo zonsezo



BOSTON UNIVERSITY
1 1719 01826 7866

adaonabe kuti adalibe nazo kanthu.

'Chofunika apa ndi ntchitoyo basi,' Mateyo ankatero mumtima mwake. Maganizo ake adalidi anzeru. Tsiku lina masana nthaŵi yopumula, Mateyo ndi anthu ena adakhala pansi pa mtengo wa malaina pomwe padali mthunzi. Pamenepo pankabuka nkhani zosiyanasiyana. Zina za ku ntchito, zina za m'tawuni momwemo, zina za m'mabanja. Konseko kudali kupititsa nthaŵi kuti akalowenso chigawo china chomaliza tsiku limenelo.

"A Bwezani ndiye munthu mmodzi woipitsitsa pa kampani pano," wina adayamba nkhani.

"Chifukwa 'chiyani?" adafunsa Mateyo ncholinga chofuna kudziŵa zambiri.

"A Bwezani kaŵirikaŵiri amangokalipira munthu popanda chifukwa chokwanira ndipo achotsetsa anthu ambiri ntchito pano," adatero.

"Kanitu amalakwa chifukwa ntchito ndiwo moyo wa munthu. Kuchotsetsa mnzako ntchito n'chimodzimodzi kuchotsa moyo wake. Anthu ambiri amavutika chifukwa cha munthu wochotsedwayo. Choncho kutero sibwino, chifukwa nthaŵi zina Mulungu amalanga," adatero Mateyo.

"Nanji akadziŵa kuti ndi ophunzira ngati inuyo ndiyetu basi," adapitiriza mkuluyo.

"Mukundiuza kuti iwoŵa sadaphunzire?" adafunsa Mateyo.

"Kuphunzira komwe kothawira pa windoku."

"Mwatero? Nanga mpando wa umaninjala adaupeza bwanji?"

"Ekesipiriensi achimwene. Pantchito pano akhalitsa. Zaka makumi aŵiri mwati nkukhala chibwana?"

"Eee. Eeedi zoona akhalapo. Chomwechotu ndiye bwino. Mwalatu wogudubuka suyanga ndere."

Nthaŵi yoyamba ntchito itakwana, onse adabalalikira mmalo mwawo. Mateyo mwezi womwewo adalemba kalata yopita kumudzi kwa amayi ake aang'ono Alekenianene, kuŵalongosolera momwe adayendera. Adaŵadziwitsanso za nkhani yoti tsopano adayamba ntchito.

Mwezi wachiŵiri, Mateyo adayamba kuzindikira zina zoipa za a Bwezani. Tsiku lina Mateyo akutsuka makapu ku khitchini, a Bwezani adamuitana.

"Kodi iwe Mateyo!"

"Bwana!"

"Osamangoti bwana uli chikhalireni. Tabwera kuno msanga!" adakalipa a Bwezani.

Nthaŵi yomweyo Mateyo adasiya ntchitoyo kuthamangira ku ofesi ya a Bwezani.

"Ndabwera bwana," adatero Mateyo, ali wefuwefu kupuma.

"Ndagula ndiwo izi zili m'pepalazi tsono ukatule kunyumba. Ufulumire wamva?" adalamula a Bwezani, mokalipa. Nthaŵi yomwe Mateyo ankatuluka mu ofesiyo, adamenya thenifolo kunyumba kwa akazi awo, ati kuŵadziŵitsa nthaŵi imene Mateyoyo adachokera ku ofesiyo. Mateyo adathamanga. Nthaŵi yomwe ankakafika kunyumba idali zitatha mphindi 30 chifukwa udali mtunda wautali ndithu.

"Odi odi!" adaodira Mateyo kunyumba kwa bwana.

"Eee. Loŵani," adayankha akazi a Bwezani.

Mateyo akungoloŵa m'nyumbamo adamva mawu. "Wachedwa ndi chiyani boyi?" adafunsa Mayi Bwezani.

"Pepani mayi ulendowu ndiwautali kutereku ndimathamanga," adadandaula Mateyo.

Mopsa mtima a Mayi Bwezani adangolandira motsomphola ndipo osapereka ndi zikomo yemwe, basi, namuuza kuti akhoza kubwerera ku ntchito.

"Ufulumiretu chifukwa bwana wako akukuyembekezera!" adamuuza.

"Zikomo Madamu." Mateyo ankavomera akuthamanga.

"Bwanji watenga ola lathunthu kukafika kunyumba?" nawonso bwana Bwezani adakalipa ku ntchito.

"Mwamva ndani bwana kuti ndatenga ola lathunthu kukafika kunyumba?" adafunsa Mateyo, thukuta lili kuno, kupuma kwake kwa wefuwefu ngati mbawala yothawa lupsa la moto.

"Usandifunse funso chomwecho ngati iweyo uli ndi udindo wina uliwonse pano! Ndikhonza kukuchotsa ntchito ine!" Adakalipa a Bwezani.

Mateyo adasoŵa chonena. Ankangoŵayang'ana a Bwezani akulalata. Adamuuza kuti akapitirize ntchito yake. Adanyamuka Mateyo. Akungofika pa khomo, adamuitana kuti abwere nkumuuza kuti akaŵapangire tiyi msangamsanga. Atatha ntchito yonse chifukwa chotopa Mateyo adati awongolepo msana. Nthaŵi yomweyo a Bwezani adatulukira.

"Panopa ukuchita chiyani? Ukungonyenya eti?" adakalipa.

"Ayi bwana koma kuti ndimati ndiwongole msana."

"Msana, msana wachiani? Msana umagwira ana ngati inu?" Mateyo sadayankhe. Adangogwetsa nkhope yake pansi. Kukhala kwa a Bwezani kudali kumeneko nthaŵi zonse. Aliyense pamalopo ankasimba nkhani ya a Bwezani. Komabe Mateyo adapirira kufikira chaka chidatha.

Mutu 6

## Pano mpakachere

Tsiku lina Mateyo ataŵeruka ku ntchito madzulo, adakumana ndi anzake ena akupita ku sukulu. Mateyo adachita nawo chidwi anzakewo ndipo adaŵafunsa njira yomwe nayenso akadachita kuti apeze nawo mwaŵi wokaphunzira. Anzakewo adamulongosolera zonse. Atayesa njira imeneyo, malo ku sukulu adapezeka koma inkafunika ndi ndalama. Mateyo adaganiza zokapempha kwa bwana Bwezani ngati kudali kotheka kuti atapeko malipiro ake ncholinga chofuna kupeza sukulu fizi.

Mmaŵa kutacha, Mateyo, adapita ku ofesi ya a Bwezani.

"Bwana, ine ndinaganiza zophunzira sukulu ya madzulo mu Diploma ya Pabuliki Administreshoni. Ndiye ndimadzapemphako kuti nditapeko malipiro anga kuti ndikalipire sukuluyo," adapempha Mateyo ndi mawu odekha, aulemu komanso modzichepetsa pamaso pa bwanawo.

A Bwezani mmalo momuyankha m'njira yoyenera, adamufunsa. "Kodi cholinga chako nchofuna kudzatilamula ife eti?" adaonetsa kusalabadira ndi mawu a Mateyo. Nthaŵi imeneyo Mateyo adangoima potero, manja atapindira pachifuwa, popeza adalibe mwaŵi woti nkukhala pa mpando mu ofesimo ngakhale mipando yokhala alendo idalipo. A Bwezani ankafunsa funsolo maso awo ataponya kotero. Kenaka ali pa telephoni gwi, kuyimbira chibwenzi chawo chomwenso nthaŵi imeneyo chimagwira ntchito m'tawunimo. Mateyo adasowa choyankha ndi funsolo. Adaganiza kuti mwina pempho

lake lidali losamveka, mwina lidali lopanda phindu. Anadandaula Mateyo mumtima mwake. Adavutika Mateyo. Manyazi pang'ono adamugwira. Chisoni chidafungatira mtima wake. Mkwiyo udamanga phukusi m'chifuwa mwakenso. Ndi diso lotuwa la mbuu, adaliponya kwa a Bwezani.

"Bwana, sindicho cholinga changa ayi koma..."

"Basi ndamva ndidzakuyankhabe mtsogolo muno!" Atatero a Bwezani adaponya maso awo pawindo nkumangoyang'ana timadona tomwe tinkayenda mu msewu nthaŵi imeneyo.

Mateyo podziŵa kuti kanthu kali n'khama, adayesetsabe kulankhula, koma kudali kulimba mtima kokhakokha.

"Kaya ndibwerenso liti bwana kudzamva zotsatira?"

"Kodi iwe chifukwa chiyani ufuna kulimbana ndi ine pano? Ikakhala fomu fili kaya fomu folo ndi yako! Pano sitidakulembe kuti udzakhale kalaliki ayi, koma mesinjala kapena ofesi boyi, basi. Ngati sukufuna ntchito utha kusiya tilembanso wina!" adakalipa.

Mateyo adamva chinthu china kudzamuima pa khosi. Misozi idayamba kuyengeza m'maso mwake. Adausitsa moyo. Mkati mwa chifuwa mwake mudadzala mkwiyo koma sadaonetsere poyera pamaso pa bwanawo.

"Ndiye ndimati ndikamachoka pano mwina ndikhale nditadziŵa chenicheni bwana?" anadandaulabe Mateyo, tsopano kuyendera Yobu 13:13 "Chofika chindifikire".

A Bwezani adamuyang'ana Mateyo momukweza ndi kumtsitsa. "Ndanena kuti ndine munthu wotanganidwa kwambiri ndi zinthu zofunika pa kampani pano. Lakoli sidandaulo loti ndisoŵe nalo mtendere. Ndati basi pita ndidzakuyankhabe," a Bwezani adalankhula ndi mawu okweza ngati ankalankhula ndi gonthi koma chili chipongwe.

Mateyo adakhumudwa. Podziŵa kuti m'chiwuno mwa mwana simufa nkhuku, Mateyo adangobwerera pambuyo ali munthu wosadziŵa chenicheni chochita. Kudali ngati kuvundikiridwa m'dengu ngati nkhuku yachilendo.

Mateyo adadziŵa kuti chabwino palibe. Zinthu zidaipa basi. Komabe iye sadasiyire pomwepo ayi. Adalimba mtima kupita kukapereka chidandaulo chake kwa bwana Sikoti amene adali wamkulu pa kampaniyo (Genolo Manijala). Atafika pa ofesi yake adagogoda nalowa. Adampempha kuti akhale pampando.

"Ndikuthandizeni chiyani a Mateyo?" adafunsa m'chingelezi bwana Sikoti. Mateyo adapeza phuma kuti alankhule chifukwa cha mantha. Kenaka adalimba mtima nayenso nayamba kuchikulumunya chingelezi ngakhale chidali chophophonyaphophonya. Zonsezi zidachitika chifukwa cha mantha.

"Ine bwana ndabwera ndi vuto loti ndimafuna kumachita nawo maphunziro a madzulo a Diploma ya Adiminisitreshoni ku Baadya Koleji, ndiye ndimapemphako kuti nditapeko malipiro anga ndilipirire sukuluyo," adatero Mateyo.

"Bwanji vuto limeneli sudauze a Bwezani kuti akuthandize?" adafunsa mzungu.

"Ndinapitako ku ofesi kwawo kukadandaula."

"Ndiye iwo ati bwanji?"

"Angondiuza kuti adzandiyankhabe. Koma popeza masiku olipira atsala pang'ono kutseka, ndicho chifukwa chake ndabwera kwa inuyo bwana kuti mwina mungandithandize mofulumirapo."

Pamenepo mzungu uja adati chete choyamba osayankha msanga.

"Kodi paja takhala nawe kwa nthaŵi yaitali bwanji?"

"Chaka ndi miyezi itatu bwana."

"Sukulu paja udasiyira fomu chiyani?"

"Fomu fili bwana!"

"Ndiye pano ntchito yako umagwira yotani tsopano?"

"Ndine mesinjala ku ofesi ya bwana Bwezani."

"Eeeee. Chabwino. Tsopano umafuna kutapa ndalama zingati?"

"Ndimafuna kutapako hafu kuti hafu ina yotsalayo ndidzalandire kutha kwa mwezi."

"Chabwino izo ndamva. Ukatenge mafomu a zango-

ngole ubwere nawo kuno ndidzakusayinire. Tsopano maŵa ubweretse satifiketi yako ya J.C. ndidzayione, wamva?"

"Inde bwana ndibweretsa. Zikomo kwambiri mwandithandiza."

Mateyo adatuluka muofesi chisangalalo chili tsaya. Adakatenga ma fomu aja. Atatha kulemba pa mafomuwo adathamanga nawo kwa mzungu uja. Zonse zidakonzedwa tsiku lomwelo.

Nthaŵi yomwe Mateyo ankatuluka mu ofesi ya mzungu muja, a Bwezani adamuona ndipo adamuitana mosonyeza kuipidwa.

"Iwe Mateyo tabwera kuno msanga!" Kuitana kwawo kudatsimikiza mkwiyo umene udali m'chifuwa mwawo.

Mateyo adapita kumeneko. "Ndabwera bwana!"

"Kodi ku ofesi ya Sikoti ija umakachita chiyani?"

"Ndimakalongosola vuto langa lomwe lija bwana."

"Vuto, vuto lamtundu wanji?"

"Lomwe lija la sukulu bwana."

"Kodi Mateyo wayamba kundionera mkoodi iwe eti? Zija ndinakuuza dzulozi sudakhutitsidwe nazo? Kodi ukudziŵa kuti ineyo ndili ndi mphamvu yokuchotsa ntchito pano ndipo bwana ukuti bwana wakoyo kwake nkungovomereza basi? Pano ukusiya ntchito, nkumakaseŵera panja?" adakalipa a Bwezani, diso lili kuno.

"Pepani bwana. Kodi nanga ndikadachita chiyani?" adapepesa Mateyo.

"Nyonyonyo bwana! Ukuyesa ine mpando uno ndingakhalire za maseŵera ngati zimenezi eti? Udzawonjezenso, ndiye kuti ntchito yako idzaumira pomwepo ndilibe za masanje ine. Basi pita!" adakalipa.

Chifukwa chokalipiridwa chonchi, mtima wokonda ntchito udachoka mu mtima mwa Mateyo. Kunja kunkati kukacha, kukhosi kuti bii. Nthaŵi yoŵeluka ikakwana ankachita kuutsitsa moyo kuti tsiku limenelo lapita.

Ndiye mmaŵa wa tsiku linalo Mateyo sadayiwale kutenga satifiketi yake ija poganiza kuti mwina zinthu zidzayenda bwino.

"Bwana ndikupita ku ofesi ya bwana Sikoti, anandipempha satifiketi yanga, kuti ayione," adalawira Mateyo.

"Pita kwa bwana wakoyo." Adayipidwa a Bwezani.

Mateyo adapita. Adampatsa bwana satifiketiyo. Atalandira Bwana Sikoti adaonetsadi chidwi. "Basi pita kagwire ntchito, tiganizira njira ina," adatero bwana Sikoti.

Kuyambira tsiku limenelo, Mateyo tulo sitinkabwera konse usiku m'maso mwake. Ankangoti gadabugadabu pa mphasa usiku wonse ngati nsomba ya mlamba m'madzi. Tulo nthaŵi zina tikabwera, maloto ake ankakhala omuzunguza maganizo okhaokha. Tsiku lina Mateyo adalota akuwedza nsomba za chambo. Atafotokoza za malotoŵa kwa wina yemwe adamuuza kuti ndi mwaŵi, sadathe kukhulupirira. Adafunsanso wina. Adamuuza chimodzimodzi.

"Ukalota ukupha nsomba za mlamba limakhala tsoka. Koma ngati ndi chambo, mwaŵi umenewo," adamutsimikizira mkulu winayo.

"Osati ndi maloto chabe amenewo?"

"Ayi mkulu mwaŵi basi."

"Ayi tiona ndithu."

Tsiku lina Mateyo akungobwera ku ntchito mmawa adakumana ndi a Bwezani.

"Mateyo undipeze ku ofesi posachedwapa. Yunifolomu usavale msanga," adamuuza a Bwezani.

"Chabwino bwana," adayankha Mateyo naganiza kuti basi, ntchito yake idatha. Nkhongono zonse zidazizira. Ankangonjenjemera. Mu ofesimo, kwa nthaŵi yoyamba, Mateyo anadabwa kumva a Bwezani akumuuza kuti akhale pa mpando.

'Ndizoona zimenezi, Kwagwanji lero?' Mafunso ambirimbiri adabadwa mmutu mwake. Mateyo adakhala pampandopo. A Bwezani adatulutsa failo yake n'kuika pa tebulo.

"Mateyo, kuyambira lero lino wakwezedwa kukhala kalaliki. Ndipo uzikhala ofesi inayo. Wamva?" adatero a

Bwezani.

"Zikomo bwana," adathokoza Mateyo.

A Bwezani adatulutsa kalata yomwe idachokera kwa bwana wamkulu, bwana Sikoti nkumupatsa Mateyo. Atalandira adaitulutsa mu inivilopi, nkuyitambasula. Adaŵerenga mofatsa.

Okondeka Mateyo Taonana,

**Kukwezedwa pa Ntchito**

Tikuthokozani chifukwa chokwezedwa pa ntchito kuchokera pa Mesinjala kufika pa Kalaliki.

Kuyambira tsiku la lero mtengo wanu pa mwezi udzakwezedwa ndi 50 kwacha.

Tikhulupirira kuti mudzalimbika kugwira ntchito monga mwakhala mukuchitira mmbuyomu.

Zikomo.

Sikoti
Genolo Manijala

M'maso mwa Mateyo mudachita misozi, osakhala ya chisoni koma yachimwemwe.

"Wamaliza kuŵerenga eti?"

"Inde bwana."

"Tsopano wakondwera kuti ndiwe kalaliki eti?"

"Inde bwana."

"Nanga sukulu yako ija upitirizabe?"

"Inde bwana ndipitiriza."

"Eeee. Ndiyetu ufuna kudzatilamula eti?"

"Ayi bwana osakhalanso zimenezi."

"Tsopano ukufuna kudzivutiranjinso?"

"Basi kungofuna kupeza nzeru."

A Bwezani adaonetsa mtima wosasangalala kwenikweni. Ngakhale izi ankamuuza kuti wakwezedwa pa ntchitopo, ankachita izi chifukwa choti iwonso adachita

BOSTON UNIVERSITY
19 01826 7866

kutumidwa ndi bwana Sikoti. Mkati mwa mtima mwawo mudali moto woyaka, komabe panalibe njira ina iliyonse yomwe a Bwezani akadatha kuchita.

Mateyo adatuluka mu ofesimo ali munthu womasuka tsopano. Adayamika Chauta chifukwa cha zabwino zonse.

Mateyo sadasiyedi sukulu. Ankati akaŵeruka ku ntchito, madzulo, basi ulendo ku sukulu. Mwaŵi adali nawo Mateyo. Kampani idamuuza kuti idzamubwezera ndalama zake zonse ngati adzakhoze mayesowo.

Chifukwa cha khama pa maphunziro, zotsatira za mayeso zitabwera, Mateyo adakhoza bwino ndi muja amati kukhoza ndi 'Distinkishoni' Adalumpha ndi chimwemwe Mateyo tsiku limenelo. Mateyo podziŵa kale za moyo wa a Bwezani, choyamba adapita ku ofesi ya bwana Sikoti. Nkhaniyi adasangalala nayo bwana Sikoti ndipo adamulonjeza zambiri Mateyoyo. Ndalama zake zonse zidakonzedwa kuti amubwezere.

Mmaŵa wa tsiku linali, nkhani ya kukhoza mayeso kwa Mateyo idamveka pa kampani ponsepo. Ena osinjirira ankati Mateyo adzatenga mpando wa a Bwezani. Koma mbiri yotereyi Mateyo sankakondwa nayo popeza ankadziŵiratu zotsatira zake. A Bwezani atamva kuti Mateyo wapambana mayeso, mtima wawo udaŵapweteka. Adayipidwa nayo nkhaniyo.

"Mwana ameneyu akufuna kundiposa ine eti?" Adavutika mumtima mwawo. Ndiye kuyambira pamenepo, a Bwezani adakhala akumulondalonda m'mapazi Mateyo kuti ampezere chifukwa. Kaŵirikaŵiri ankampatsa dala ntchito yovuta. Mmalo moti akalandira ntchito yachilendo yofunika onse kuikhalira pamodzi kulongosolerana choyenera kuchita, a Bwezani ankangomuunjikira ntchitoyo Mateyo. Ndiye poti ntchito yosaidziŵa akachedwetsa kumaliza, ankakhala mavuto. Chimene iwo ankachita zikatero a Bwezani nthaŵi yomweyo ankathamangira kwa bwana Sikoti kukapereka malipoti omuipitsa Mateyo.

Tsiku lina mwaŵi wa a Bwezani udapezeka. Usiku wapitawo kunyumba kwa Mateyo kudabwera akuba

nkumubera katundu wake. Mmaŵa kutacha Mateyo adapita ku Polisi kukapereka sitetimenti.

Nthaŵi yomwe Mateyo ankabwera ku ofesi idali 10 koloko mmaŵa. Atamuona a Bwezani, adamuitana. Mateyo adapita.

"Chifukwa choti anzathu ndinu munthu wophunzira, mwakwera pa ntchito, basi mwayamba kunyoza ntchito eti? Ndiponso ntchito ukulephera. Nthaŵi zonse kubwera ku ntchito ukungobwera mmene uganizire. Uli gwede, gwede, gwede, ngati ukupita kuchitsime. Kodi ntchitoyo ya agogo ako, ya ndani ukuinyadirayi?" adakalipa monyogodola a Bwezani.

Nthumazi idamuomba Mateyo kuti phii. Thupi lake lidachita mantha. Mtima wake udagunda kwambiri.

"Bwana, bwanji mundifunse choyamba chimene ine ndachedwera kubwera ku ntchito?" anadandaula Mateyo.

"Ndiribe nthaŵi yokufunsa zimenezo. Koma ineyo, ndikuti ntchito yako yatha basi."

"Bwana ndiye kuti...

"Bwana ... Bwana... chiyani? Basi ineyo ndikatero ndiye kuti zonse zatheka. Bwana Sikoti wakoyo wauzidwa kale za khalidwe lako. Basi yauma mkulu."

"Kodi chifukwa chake ndi chomwechi?"

"Ndati usandifunse mafunso chifukwa kuno sikukhoti ayi." Nthaŵi yomweyo a Bwezani adaimirira kukhala ngati kuti ankafuna kutulukamo mu ofesimo. Mateyo adangoima phee. Sadafunenso kulimbana nawo. Misozi idayengeza mmaso mwake, koma asanatuluke mu ofesimo adati:

"Bwana, ine lero mwandichotsa ntchito. Zikomo kwambiri. Ambuye akudalitseni. Chachikulu dziŵani kuti, pano mpakachere pokoma kudyerana. Muyeso womwe umayesa nawo wina, udzayesedwanso ndi womwewo. Ndapita..." Mateyo adatuluka mu ofesimo kupita ku ofesi ya akauntsi kukalandira ndalama zake.

BOSTON UNIVERSITY
19 01826 7866



## Chaona mnzako chapita maŵa chili pa iwe

Sipadatenge masiku ambiri Mateyo asanapeze ntchito. Kuchotsedwa kwake ntchito ku kampani ya Simbani Zatha kudampatsa mwaŵi wina wapadera. Pomwe sabata imodzi inkatha, makampani angapo adali atamuitana kuti akayambe ntchito. Pamenepo Mateyo adachita kusankha kampani yomusangalatsa. Iye adakayamba ku Dzaoneni Kampani. Mateyo adasankha kumeneko osakhala chifukwa chakuchuluka kwa malipiro okha, koma chifukwa cha nyumba yaikulu imene adamupatsa kudzanso maphunziro akunja. Adamulonjeza kuti akadzamaliza chaka chimodzi, kampani idzampatsa mwaŵi wokachita maphunziro ku Mangalande.

Anthu ogwira nawo ntchito ankampatsa ulemu Mateyo, pobwezera khalidwe lake labwino.

'Munthu ukayamba nkuvutika nthaŵi zina, umamalizira ndi ubwino', ankaganiza Mateyo mumtima mwake. Chisangalalo tsopano chidaali tsaya. Ku Dzaoneni Kampani adalembedwa ngati wachiŵiri kwa Pelesonelo Manijala, ndipo Pelesonelo Manijala weniweniyo adali Mzungu dzina lake Symoni. Zimenezi zidaonetseratu poyera kuti mtsogolomo Mateyo adzatenga mpandowo pamene Symoni adzapita kwawo. "Sunga khosi mkanda woyera udzavala," anthu ena ambiri ankamulimbitsa mtima Mateyoyo.

Chifukwa cha mtendere wa mumtima mwake pa ntchito, Mateyo ankagwira ntchito mosangalala. Iye adadziŵa kuti zonse sizibwera tsiku limodzi. Adaganiza mwambi uja wonena kuti, tsiku limodzi siliwoza mbeŵa.

Chaka chimodzi chitatha, kampani idampezera malo ku Mangalande kuti akachite maphunziro ake kumeneko. Zonse zaulendo wake zidayenda bwino ndipo adanyamuka ulendo wa ku maphunziroko.

Pa Dzaonenipo, aliyense wogwira ntchito adakondwera kuti Mateyo adapita ku Mangalande kuti mtsogolomo zonse zikadzayenda bwino adzatenge mpando wa bwana Symoni. Adamfunira mafuno abwino Mateyo. Zonsezo zinkachitika chifukwa choti Mateyo adali munthu womva dandaulo la anthu pa kampanipo. Ngati munthu alowa mu ofesi mwake, asanafunse chilichonse choyamba ankampatsa mpando kuti akhale, basi nkumamfunsa bwino. Mateyo sadafune kubwezera choipa ku choipa poganizira za a Bwezani ayi koma chabwino ku choipa.

Mateyo ku Mangalande adakathako zaka zinayi ndipo uko adakabwera ndi Digiri mu Pabliki Adiminisitireshoni. Atafika kumudzi adakwatira mkazi wophunziranso dzina lake Napungani.

Zaka zinayi ku Mangalande idali nthaŵi yaitali ndipo zinthu zambiri zidachitika mmbuyo mwake.

Chinthu chimodzi chimene chidafuna kumuliritsa Mateyo chidali kumva kuti nthaŵi yomwe Mateyo adangopita ku Mangalande, a Bwezani, ku Simbani Zatha kuja ntchito yawo idatha chifukwa chowononga ndalama za kampani.

Ntchito ya a Bwezani itatha, adamangidwa zaka zitatu. Mateyo misozi idayengeza m'maso mwake. Chisoni chidamugwira.

Mateyo atafika kunyumba kuchokera ku ntchito sadasangalale tsiku limenelo.

"Dadi, muwoneka kuti ndinu munthu wosasangalala lero. Kodi mwatani?" adafunsa Napungani, mkazi wake atakhala chapambalipa.

Mateyo adapukusa mutu, namuyang'ana Napungani kunkhope. Kanthaŵi pang'ono kanadutsa aŵiriwa akungoyang'anitsana.

"Zochitika pa moyo wa munthu ndizambiri," adala-

BOSTON UNIVERSITY
19 01826 7866

nkhula Mateyo.

"Bwanji?" adafunsanso Napungani.

"Basi ndamva nkhani yondivuta ,m'maganizo. Paja ukudziŵa kuti nthaŵi zina ndidaali ku kampani ya Simbani Zatha?"

"Eya ndidamvapo."

"Kumeneko kudaali mkulu wina dzina lake Bwezani. Adali bwana wanga. Ameneyo ndiyemwe adandichotsa ine ntchito popanda chifukwa chokwanira.

Komanso a Bwezani adachotsetsa anthu ambiri ntchito pomanena ugogodi woyipa kwa Genolo Manijala. Inenso adachita chimodzimodzi."

"Ndiye...?"

"Basi akuti ntchito idaŵathera komanso adamangidwa zaka zingapo."

"Tsopano mukumva chisoni ndi mfitiyo bambo?"

"Inde. Akuti usabwezere choyipa koma kumafunirana zabwino nthaŵi zonse. Wachifundo adzalandira chifundo."

"Haa, ine ayi sindingachite chifukwa iyeyo ndi mfiti, mthakati wachabechabe. Munthu wosafunira mnzake mafuno abwino ndi wosafunika pa chitukuko cha dziko. Anthu ena amaiŵala kuti ntchito ndiyolembedwa iwonso pangapite nthaŵi yotalika bwanji, tsiku lina adzachotsedwa."

Mateyo sadaonetse nkhope yogonja. Chisoni chidakulabe mumtima mwake. Patatha zaka ziŵiri, bwana Symoni adabwerera kwawo. Mateyo ndiamene ankagwirizira mpando wake.

Tsiku lina adalandira kalata yoti adakwezedwa kuloŵa m'malo a bwana Symoni. Ndalama adamuonjezera zambiri. Nyumba adampatsa ina yaikulu ku mayadi komwe kunkakhala bwana Symoni. Adampatsa galimoto kuti adziyendera. Lidali tsiku lachikondwerero... Akutitu, chaona mnzako chapita maŵa chili paiwe.

Lidali tsiku Lachisanu masana dzuŵa likuswa mtengo. Kumwamba kudalibe ndi mtambo womwe. Mpheponso kudalibe. Anthu ogwira ntchito m'tawuni

ankapumula m'mithunzi kuphwetsa mkhuto wa masana. Ena ankayenda bawo, mbali inayo ena akuseŵera makadi. Konseko kupititsa nthaŵi kuti akayambenso chigawo china chotsiriza tsiku limenelo.

Pa mthunzi, pa mtengo wa bulugama potero anthu enanso adasonkhana. Ankamvera mawu a M'bukhu Loyera. Nyimbo zokoma za Mulungu ndi ulaliki zidali kufalitsidwa.

Idali nthaŵi yomwe a Bwezani nawo adatopa chifukwa choyendayenda m'tawuni kupita akufuna ntchito. Nthaŵi yomwe adamva kuimbako, mtima wawo udasonthoka. Thukuta ankachita lokomba, milomo itatuwa gwa, ndi njala ya chichereni. Adapita malo amenewo kuti akadzimvere okha, poganiza kuti Chauta angaŵatsogoze mwapadera. Kuyenda kwawo kudaonetsa kuti analidi wotopa. Adaoneka munthu wopanda mphamvu. Adaoneka munthu wosowa mtendere mu mtima. Mavuto osiyanasiyana adamanga kachisi pa thupi lawo. Atayenda apa ndi apo m̃tawunimo kwa miyezi yochuluka, a Bwezani adataya chikhulupiriro choti nkudzakhalanso pa ntchito. Chiyembekezo chawo chidali imfa basi.

Nthaŵi yomwe ankafika pa malopo adapeza mlaliki ali mkati kulalika Uthenga Wabwino. Adaonetsa chidwi kuti amvere. Maso awo adaponya kwa mlalikiyo yemwe anali kulumpha nawo uthenga. Iyeyo ankati akayenda napita uku kenaka nkubwerera pambuyo, manja atatambasula moimika kumwamba, anthu omverawo ankangopukusa mitu. Kudali kukanda posayabwa akuluakulu.

"Okondedwa mwa Ambuye," adatero mlalikiyo manja ataimika m'mwamba. "M'masiku otsiriza anthu adzakhala odzikonda. Kudzakhala kudana pakati pa mitundu yonse ya pa dziko lapansi. Koma okondedwa anga, Baibulo litiuza kuti; kondanani wina ndi mnzake monga Khristu adakonda dziko lapansi. Ngati wina anena kuti akonda Mulungu nadana ndi mbale wake ali wabodza!" adapuma kaye pang'ono namwaza maso ake ku gululo. Analidi masana aphindu, masana achitsitsimutso. Adayenda pang'ono kutsogolo, nabwereranso pambuyo

BOSTON UNIVERSITY
719 01826 7866

kenaka nkudzayang'ana kumwamba. Pamene adagwetsa nkhope yake pansi zidali ngati kuti mawu ena adachokera kumwambako oti auze anthu omverawo.

"Chikondi chiposa zonse. Chikondi chilibe ndewu, kudzikweza, njiru, miseche, ufiti, kaduka, nkhondo. Koma chikondi chimamkonda mnzake monga iye mwini." Pamenepo adalasadi m'mitima mwa anthu ambiri. Ena adavomerezana nawo mawuwo. Ena adalankhulapo mawu onyodola. Kumeneko ndiye kukhala kwa munthu.

"Kodi anthu inu mufuniranji madalitso ochokera kumwamba pamene muli anthu okanika kumvera Mbuye wanu amene adakulengani? Mufuniranji chifundo pamene muli anthu osoŵa chifundo kwa anzanu? Abale, mudziyesere nokha m'chikhulupiriro chanu chifukwa tsoka kwa iye amene achita izi nkusaŵeruzika popeza ..." anadukiza nameza mate kaye. Nthaŵi imeneyo maso ake adangophuthira.

Kenaka ndi mawu odekha apansi adati, "Mphotho ya tchimo ndi imfa. Tiyeni tonse tipemphere." Adapemphera.

A Bwezani adangoti pakamwa kakasi. Mawuwo adaŵagunda kwambiri mumtima. Adadzimvera okha chisoni. Chikumbumtima chidaŵapeza. Adakumbuka za masiku amenewo. Ndiye monse ankachoka pa malo amapempherowo, a Bwezani adali munthu wokhumudwa. Mphamvu za satana zidaonekera poyera kwa iwo. 'Choipa chitsata mwini ...' adaganiza mozama a Bwezani mmenemo akupita poteropo m'tawuni ya Onani, kuloŵera msewu wa Mwaziwona Avenue.

A Bwezani akuyenda mu msewumo, adakumana ndi munthu wina amene adasonyeza kuŵazindikira.

"Muli bwanji bambo Bwezani?"

"Ndili bwino kaya ndiope inu," adayankha a Bwezani koma modabwa.

"Inenso ndili bwino. Mwinatu mwandiyiwala eti? Dzina langa ndine Kachule. Tidali limodzi ku Simbani Zatha. Mwandikumbukira tsopano?" adadziwulula mkuluyo.

"Indedi, eya ndinu a Petulo Kachule? Indedi eeti taonani. Ndiyetu mukupeza bwino anzathu?" adamzindikira tsopano. Timanyazi tidaŵagwira a Bwezani.

Petulo Kachule adali mmodzi mwa anthu amene a Bwezani adaŵachotsa ntchito ku Simbani Zatha popanda chifukwa. Koma lero Kachule adali kugwira ntchito ku kampani ina m'tawuni momwemo. Ntchitonso yapamwamba osakhala ngati ku Simbani Zatha.

"Osanamadi bambo, ine masiku ano ndikudya bwino. Munthu uyenera kukhala wothokoza chimene Mulungu wakupatsa, ndiye amakuonjezera zina osati wosuliza ayi," adatero Kachule. "Nanga ulendowu mukupita kuti bambo?" adafunsa Kachule.

A Bwezani sadayankhe msanga. Kenaka adati: "Achimwene ndikuyesayesa kufuna maganyu m'tawuni muno. Pajatu ku Simbani Zatha zinthu zidavutapo," adatero a Bwezani.

"Pepani bambo. Mwina mutayesa kulowera chapamunsipa chifukwa ndinamva kuti kampani ina ikufuna anthu. Mwina mungakapezeko mwaŵi kumeneko," adaŵauza Kachule.

"Achimwene, mwachita bwino mwandilangiza ndiyenera kupita kumeneko. Sindingathe kudziŵa kuti mwaŵi wanga wa ntchito ungachokere pamenepo," adayankhula mothokoza.

Atatha kukambirana zina ndi zina adasiyana. A Bwezani adalondola msana wa njira kupita kumeneko. Atafika pa ofesi ya bwana wolemba anthu ntchito, adagogoda pa chitseko.

"Lowani," adayankha mawu achikazi. Adalowa. Adampeza mzimayi ali wotanganidwa kumenya taipi. Adali wodziŵa kulandira alendo. Atangoloŵa, nthaŵi yomweyo adaŵapempha kuti akhale pa mpando. Adasiya kaye ntchito naŵapatsa moni. "Nanga tikuthandizeni bambo?" adaŵafunsa mwaulemu. A Bwezani adamuyang'ana mayiyo.

"Inde ... bwa... madamu..." adajejema polankhula. Adati aziimirira pa mpandopo koma mayiyo adaŵaletsa.

Kenaka a Bwezani adalimba mtima.

"Ndikufuna ntchito madamu," adatero kwina akuti azitulutsa makalata awo a ntchito kuti amuonetse mayiyo.

"Musavutike bambo ndi kutulutsa masatifiketi anu popeza ntchito ilipo ndi ya ulebala basi," adatero mayi uja. A Bwezani adabwezeretsa mapepala aja mu enivolopi.

"Mudzaikonda ntchitoyo bambo?"adaŵafunsa mayi.

"Mayi musadandaule ndi zimenezo chomwe ine ndifuna ndi ntchito basi."

"Chabwino dikirani pang'ono chifukwa a Pelesonelo Manijala ali ndi anthu ena."

"Zikomo kwambiri mayi," adathokoza a Bwezani kenaka nkusetekera milomo yawo ndi lirime kuti ifewe. Adayembekeza a Bwezani, mtima wawo ukugundagunda mkati mwa chifuwa mwawo. Akuyembekeza chomwecho padafikanso anyamata ena aŵiri odzafunsira ntchito. Onsewo adaŵauza kuti ayembekeze pamenepo kufikira bwanawo adzalamula kuti alowemo.

Nthaŵi pang'ono munthu wina uja adatuluka ndipo mayi uja adaŵauza a Bwezani kuti aloŵe.

"Loŵani!" adamva mawu a Bwezani atagogoda pa chitseko. Modzichepetsa zedi adakankha chitsekocho, kuyenda kwawo konyang'ama ngati ankaponda matope. Kenaka adaloŵa. Koma pepani. Kudaali kudzidzimuka ndi manyazi. Kodi amalota? Adadzifunsa a Bwezani. Ndani bwana wakhala apoyo? Nthaŵi imeneyo Mateyo adali ndi chimwemwe kuŵaona a Bwezani mu ofesimo patapita zaka zambiri. Koma kumbali ya a Bwezani kudali ngati kukumana kwa mwezi ndi dzuŵa. Adagwetsa nkhope pansi. Komabe a Bwezani adadzilimbitsa mtima. Adakhala pampando koma ali munthu wosoŵa mtendere mumtima.

"Mwangotiyendera lero lino bambo Bwezani?" adafunsa Mateyo, chimwemwe chikusefukira pakamwa.

A Bwezani pakamwa padauma. Simomwe ankaganizira. Akadadziŵa kuti wolemba ntchito anthu ndi Mateyo, a Bwezani mwina sakadafika pamalopo. Pamene-

po ngakhale poyambira pamene padavuta. Komabe mapeto ake a Bwezani adalimba mtima nalankhula.

"Ndikufuna ntchito bwana. Mwana wanga ndazunzika ine, ndaziona ine, ndazigwira ine. Tsopano ndikudandaula nkhani ya ntchito pa maso panu bwana," adalankhula a Bwezani.

Mateyo sadathe kuyankha msanga. Adaŵayang'ana a Bwezani.

"Mukufuna ntchito ya mtundu wanji bambo?" adafunsa Mateyo.

"Iliyonse bwana. Ndamva kuti mukufuna anthu aganyu pano. Imeneyonso ndi ntchito. Chofunika kwenikweni ndi makobidiwo bwana," adatero a Bwezani.

"Mwatero bambo?" adayankha Mateyo.

M'maso mwake mudachita yengezi misozi. Sikuti Mateyo ankafuna kulira chifukwa choti a Bwezani adadzafuna ntchito kwa iye, koma chikumbumtima cha masiku amenewo chidayamba kumufikira. Tsopano posafuna kuti agwetse misozi, Mateyo adaphiphiritsa ndi kulankhula. "Kunena zoonadi ntchitoyo iripo koma ndi ya ulebala. Mulola?"

"Palibe chifukwa bwana," adayankha a Bwezani.

Mateyo adaŵayang'ananso kwa nthaŵi ina yaitali. Nthaŵi yomwe amatenga bolopeni kuti ayambe kulemba dzina lawo m'failo, Mateyo adadzidzimuka kuona misonzi ikugwera pa pepala.

# LINDA MADZI APITE

Mlembi wa bukhu la "Linda Madzi Apite" adabadwira m'mudzi mwa a Zamasiya ku Ntcheu. Adachita maphunziro a pulaimale ndi a sekondale ku Ntcheu komweko mpaka kupambana mayeso a Malaŵi Certificate of Education (MCE).

Atatsiriza maphunziro a sekondale m'chaka cha 1977 adagwirapo ntchito za muofesi kwa chaka chimodzi ku Manpower Assessment and Appointments Bureau (Ministry of Labour) ku Blantyre. M'chaka cha 1978 adapita ku Malaŵi Polytechnic kukachita maphunziro a Mechanical Engineering Technician kwa zaka zinayi. Potsiriza pa maphunzirowa a Mindano adalandira satifiketi ya Full Technological Certificate kuchokera ku London.

M'chaka cha 1988 a Mindano adapita ku Mohawk College ku Canada kukachita maphunziro kwa miyezi isanu ndi umodzi nalandira dipuloma mu Mechanical Engineering Laboratory ndi mu Basic Computer Programming. M'chaka cha 1989 adakhala membala mu bungwe la Board of Engineers, Malaŵi (Registered Technician Engineer).

A Mindano agwira ntchito m'malo angapo. Agwira ntchito ku Lever Brothers, ku Dwangwa Sugar Corporation ku Nkhotakota ndipo ku Malaŵi Polytechnic ndi ku Blantyre Print komwe



*Nixon D. Mindano*

adakali tsopano pamene buk
lawoli likufalitsidwa.

A Mindano ali ndi banja ndi
ali ndi ana anayi, ndipo mmo
wa iwo ndi wamwamuna.

"Linda Madzi Apite" 
bukhu lophunzitsa chikhalid
chabwino pakati pa anthu ndi
losonyeza kukhululukira e
amene adatilakwira.

Mnyamata wakhama dzi
lake Mateyo adachita zime
sianthu ambiri adakazichi
Iyeyu mkulu womuyang'anira
ofesi adamuchotsetsa ntchito c
fukwa chomudelera. Ko
Mateyo adapeza ntchito i
kwina, nakhala wamkulu. Tso
ndi ·ilo, mkulu adamuchotset
ntchito ujanso ntchito idamuth
ra. Tsono ku ofesi komwe adak
funsira ntchito kunali k
Mateyo uja. Zidachitika pamen
po ndizo nkhani ya bukhu
ŵerengani nokha.

POPULAR PUBLICATIONS

PRINTED BY MONTFORT PRESS, LIMBE